# MAFUNSO NDI MAYANKHO

Madzulo abwino, abwenzi, ndi chabwino kudzakhala pano usikuuno. Ndipo ine, momwe izi zinakhala ngati zonse zinagwera pa ine, zinali chifukwa chakuti ine ndimaganiza mmawa uno za m'bale wanga, ndi momwe ine ndimadziwira chimene misonkhano iwiri pa tsiku imatanthauza.

2 Ndipo ine—ine ndinali ndi *ssst* pang'ono pakhosi panga; ndimalalikira kwambiri. Ndipo kenako mwamsanga pamene ine ndinafika mu mzinda, chigwa ichi, denga la mkamwa laling'ono kumbuyo kuno kuchokera ku mtundu wina wa, ichi, iwo amachitcha icho, ichi kuno nyengo yakuno mu chigwa, imangochitupitsa icho moyipa ndimangokhalira kumeza nthawi zonse pamene ine ndiri kuno mu chigwa. Ndipo ndikachokapo, masiku angapo, izo zimachoka. Kubwereranso, icho chimadzabwereranso kachiwiri.

3 Ndipo ine ndinakhala ngati ndimamumvera chisoni M'bale Neville, podziwa kuti—kuti ife mwinamwake tinapita motalikira pang'ono mu njirayi kuposa momwe ena a achinyamata inu muliri, ndipo kotero ife tikuyang'ana mbali ina. Kotero ife timakhala ngati timamvererana wina ndi mzake, ndipo mochuluka kwambiri pamene masiku ayamba kuyandikira, masiku oyipa akuyandikira. Ndiyeno podziwa kuti ife tikupita tsopano, pompano, Ambuye akalola.

4 Ndipo ine ndinaganiza, inu mukudziwa, M'bale Boze adzakhala pano Lamlungu likudzali madzulo, ine ndikukhulupirira. Ine . . . Kodi munamva zimenezo? Inde, ndipo Lamlungu likubwerali madzulo. Iye ali ndi—filimu imene iye akufuna kudzawonetsa, pa mautumiki ake ochokera kutsidwa kwa nyanja kumene . . . Iye anali ndi—loto limene linabwera kwa iye zaka zambiri zapitazo, lokhudza kubwera ku Chicago. Ndipo munthu wamng'ono wosaukayo anadzimva kusweka yense nthawi ina, anati uthenga wake unali usanakwaniritsidwe. Ndipo ndinafotokoza izo kwa iye momwe Ambuye anali atakwaniritsa kale. Ndiye iye anadzamvetsa izo.

5 Kotero ndiye Ambuye anampatsa iye loto lina. Ndipo kenako pamene kutanthauzira kunabwera, anamuuza iye koti apite ndi choti akachite. Ndipo iye anapita kumeneko ndipo, mai, oh, mai, ku Kenya ndi Tanganyika ndi Uganda, ndi mafuko amenewo kumeneko, ndi zodabwitsa basi zomwe Ambuye wawachitira iwo mu utumwi wawo. Ndipo iye akufuna kuti awonetse chithunzicho, kuti angowonetsera chimene Ambuye akuchita pakati pa anthu amenewo, mafuko achi Afrika kumeneko. Ambuye akalola, mu Januware, ine ndikufuna kuti ndidzalumikizane naye kumeneko ku . . . ndi iwo pakati pa

mafuko amenewo, kwa msonkhano basi ndisanapite kumusi ku Rhodesia ndi South Africa kachiwiri.

6 Ndipo, ndiye, limenelo ndi Lamlungu likubwerali usiku, kotero mukumbukire, tsopano. Ndipo mumupempherere mwamphamvu M'bale Joseph, iye wakhala ali m'bale wamng'ono wabwino. Ine ndamuyamikira iye kwambiri, chiyanjano chake ndi zina zotero.

7 Ndiye, sabata yamawa ikubwerayi, ife tinyamuka ndiye kupita ku. . .kupita ku Southern Pines, ndipo kenako kumusi mu Columbia, South Carolina; ndipo kenako kuchokera kumeneko kudzapita ku Cow Palace, Gombe Lakumadzulo, kenako mpaka ku Grass Valley; ndi mpaka ku World Fair, ndi kudzabwerera ku Oregon kachiwiri; kenako uko mu British Columbia, ndi kwina kotero, kupitirira ndi kupitirira mpaka kumapeto kwa kugwa masamba uku. Ndiye ife tikuyembekeza, kugwa kwa masamba uku, Ambuye akalola, kudzakhala ndi misonkhano ina yowonjezera kuno, ngati Ambuye adzapereke.

8 Kenako ine ndinaganiza, ndisanachoke, chingakhale chinthu chabwino kukhala ngati kufunsa mafunso angapo. Inu mukudziwa, iwe umapeza chimene chiri m'mitima ya anthu mukafunsa mafunso. Ndipo kotero ndiye ine ndinaganiza, inu mukudziwa, usikuuno, kungokhala ndi kuyankhulana kwa mtima ndi mtima ndi—gulu laling'ono, la anthu pano, basi—kungoyankhulana ndi inu kuchokera ku—kuchokera m'mitima yathu. Nthawizina ine ndimaganiza kuti izo zimachita bwino kwambiri kuposa kulalikira ulaliki, kungokhala ngati kumvetsetsana wina ndi mzake mwabwinoko.

9 Ndife othokoza kwa Mulungu chifukwa cha zomwe tamuwona Iye akuchita sabata ino poyankha pemphero, zakhala zabwino kwambiri. Ndipo kotero ife ndi oyamikira, basi oyamikira kwambiri.

10 Ndipo tikuwona nthawi ndi nthawi yakumapeto ikuyandikira, tikudziwa kuti chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Ndipo palibe wina aliyense koma yemwe akudziwa kuti izo ndi zoona, ngati iye ali—ngati iye ali woganiza. Ife tikudziwa, ife timayang'ana kwa izo kudutsa mmibadwo, aliyense waziwona izo. Koma, inu mukudziwa, pali zambiri zikuchitika tsopano. Ife—ife tikudziwa kuti izo ndi zoona. . . sizingakhale kutali kwambiri. Ndipo tsopano mwinamwake ine ndingayankhule pa zina za izo mu mphindi pang'ono.

11 Koma tiyeni tsopano, kuti tiyambepo, tingoweramitsa mitu yathu kwa mawu a pemphero. Ndipo pamene mitu yathu ili yoweramitsidwa, ine ndikudabwa ngati muli chinachake mmitima yathu, chimene tikufuna kuti tikumbukiridwe mu pemphero pamaso pa Mulungu. Ngati izo zingakhale chomwecho, mungokweza mmwamba dzanja lanu. Iye amvetsa, Iye amadziwa zonse za izo. Basi pempho lina limene inu

mukufuna kunena, “Mulungu, ndikumbukireni ine.” Ambuye adalitse aliyense wa inu.

12 Atate athu Akumwamba, pamene ife tikubwera usikuuno kuyandikira Mpandowachifumu wachisomo uwo, umene Inu mwachisomo mwatiitanira kuti tibwere molimba mtima pamaso pa Mpandowachifumu wa Mulungu ndi chisomo Chake, kuti tidzapemphe chopempha chirichonse chimene ife tingakhale kuti tikuchisowa. Inu munatiuza ife kuti ngati tingakhale ochuluka ngati awiri kapena atatu titasonkhana pamodzi ndi kusonkhana mu Dzina Lanu, kuti Inu mudzakhala pakati pathu. Ndipo kenako chirichonse chimene ife tidzachikhumba, ngati titachipempha icho, ife tidzachilandira icho ngati tidzangokhulupirira kuti tilandira icho.

13 Inu mukudziwa zikhalidwe za tsikuli ndi zikhalidwe za mpingo ndi za anthu, ndi zopempha zathu pamaso Panu. Tsopano, Inu mwawawona manja, Ambuye. Inu mukudziwa mitima ya anthu, ndi zokhumba zawo ndi zosowa zawo. Ndipo ife tikuiwona nthawi ikuyandikira, ikusonkhana mwapafupi tsopano, mitambo yaikulu ndi kukhazikika pansi. Zinthu zimene aneneri anazikamba zaka mahandirede ambiri apitawo, ife tikuwona kuti sizinachitikepo mpaka nthawi ino, ndipo apa ife tikuziwona izo mmasiku athu omwe.

14 Tsopano ife tikupemphera, Atate, kuti Inu mupereke kwa ife madalitso awa amene ife tikupempha. Chiritsani odwala ndi osautsika. Bwezeretsani kwa Mpingo Wanu, Ambuye, mphamvu yamoyo ya Mzimu Woyera, chikhulupiriro chamoyo kuti chimene ife tikupempha ife tizichikhulupirira. Tikukhulupilira kuti tilandira icho chifukwa ndife otsimikiza kuti ndi chifuniro cha Mulungu kuti atipatse ife tisanapemphe. Ife sitikupempha molakwika, ife tikupempha pa chifukwa cha Ufumu wa Mulungu, kotero ife tikupemphera kuti Inu mupereke izo kwa ife.

15 Mudalitse kusonkhana kwathu pamodzi, abusa athu, ogwira ntchito mu mpingo, munthu aliyense, ziwalo za Thupi la Khristu zomwe ziripo. Iwo amene si mamembala a Thupi la Khristu, akusakasaka lero pobisalirapo kwinakwake, akugula chobisalira mabomba chakubwalo lakuseri, Mulungu, mulole iwo abwere pansi pa chitetezero cha Ambuye Yesu, podziwa kuti pamene moyo uno udzatha kuli Moyo kupyola uwu. Zikomo Inu chifukwa cha lonjezolo.

16 Perekani kwa ife yankho la mafunso awa usikuuno, kuti ife tikhoze kukhutitsa mtima uliwonse ndi Mawu Anu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

17 Kuyandikira kudza kwa Ambuye, ndi chitsimikizo chachikulu bwanji!

18 Ine ndimayankhula kanthawi kapitako, winawake ananena chinachake chokhudza *inshuransi*, ine ndinali ndi Amuna

Amalonda osati kale mu umodzi wa misonkhano yawo yaikulu, msonkhano waukulu wa mayiko onse. Ine ndinangopitako ku umodzi, wachigawo. Ine ndimayankhulira a Full Gospel Business Men, dziko lonse. Ndiyeno uwu—msonkhano uwu pokhala kuti unali ku Gombe Lakumadzulo, ndi otchuka onse atakhala pamenepo ochokera konsekonse mdziko, ndi . . . ovala bwino ndipo olemekezeka. Mmodzi wa iwo anati kwa ine, "Ndinamva wina akukutchulani inu 'Abusa.'"

Ine ndinati, "Inde, bwana."

Anati, "Ndinu mlaliki?"

Ine ndinati, "Inde, bwana."

Iye anati, "Inu mukuchita chiyani ndi amuna amalonda awa?"

Ine ndinati, "Ine—ine ndi mwamuna wamalonda."

"Oh?" Anati, "Ndi malonda anji amene inu mumagulitsa?"

Ine ndinati, "Chitsimikizo."

19 Iye sanandimvetsetse ine, anaganiza kuti ndimatanthauza *inshulansi*. Kotero iye anati kwa ine, iye anati, "Kodi inu muli ndi kampani yanji?"

Ine ndinati, "Kampani Yakumwamba."

Iye anati, "Ine sindikukhulupirira kuti ndikuidziwa imeneyo."

Ine ndinati—anati, "Itiyo—ndi inshulansi yamtundu wanji imene inu mumagulitsa?"

20 "Ine sindinatero," Ine ndinati, "Ine sindinanene kuti *inshulansi*, ine ndinati *chitsimikizo*."

Anati, "Inu mukutanthauza chiyani?"

Ine ndinati:

> Chitsimikizo chodala, Yesu ndi wanga!
> Oh, kulawiratu kwake kwa ulemelero Wauzimu!
> Wolandira wa chipulumutso, wogulidwa ndi Mulungu,
> Wobadwa ndi Mzimu Wake, wotsukidwa mu Magazi Ake.

21 Kotero, usiku umenewo pamene ine ndinali kudziwitsidwa pa wailesi ya kanema, ine ndinazinena zimenezo. Ndipo ine ndinati, "Tsopano, ine—ine ndiri ndi ndondomeko pano ngati aliyense wa anthu inu pano kapena kunja uko ku dziko, amene ali ndi chidwi ndi ndondomeko, ndikufuna kukambirana nanu msonkhano ukangotha. Chitsimikizo, chitsimikizo chodala!"

22 Tsopano, ine ndinaganiza, pofunsa mafunso awa, kuti izo zikhoza kundipatsa ine kuyandikira pang'ono kwa lanu—ganizo lanu. Ine ndinali ndi awiri. Ndipo pamene

ine ndimalowa pakhomo Billy ananena kuti panali enanso, koma, ndithudi, ine sindinapeze mwayi woti ndiwayang'ane iwo. Ndipo ine ndikufuna kuti ndikhale wotsimikiza kuti ndikulondola Mwamalemba ndisanaliyankhe ilo, chifukwa inu munali. . .ndikufuna kuti zikhale mwanjira imeneyo, kapena ndisanayankhe ilo. Kotero mwinamwake ine ndikhoza kuwagwira iwo kwa nthawi ina. Tsopano, limodzi mwa. . . Ndipo poyankha mafunso awa tsopano, kumbukirani, ine ndikungochita mopambana momwe ine ndingathere.

23 Ine sindimayankha mafunso kunja mmisonkhano. Ndinayeserapo izo nthawi ina ndipo ndinalowa m'mavuto. Iwo sanandimvetsetse ine. Izo zinali zokhudza Bambo Allen, kapena za umboni wa magazi ndi mafuta ndi zina zotero, mmanja ndi nkhope, kukhala umboni wa Mzimu Woyera. Ine ndinati, "Chabwino, sindikudziwa za zimenezo," ine ndinati, "Ine sindinayambe ndawonapo chirichonse cha zimenezo mu Lemba." Ine ndinati, "Koma ine—ine ndikukhulupirira kuti ndinga. . .ndikhoza kulalikira monga chonchi m'bale, ine sindingakhazikike pa zomverera. Ine ndimangolalikira Uthenga," ndi kumapitirira.

24 Ndipo kotero iwo analemba kalata, padziko lonse, "Wokondedwa M'bale Branham. . ." kotero iyo inapita konsekonse. Ndipo iwo sanamvetsetse izo basi. Ndipo ife tinawatumizira iwo matepi ndi kuwalola iwo kuti ayisewere iyo ndi kuwona ine. . .Ananena kuti ine "ndinamutsutsa mwamunayo." Ine—ine sindinatero. Ine sindinamutsutse konse m'bale aliyense. Nthawi zina ndikhoza kusagwirizana nawo, koma izo ndi zapa ubwenzi.

25 Ndipo kenako kuno osati kale mwamuna analemba bukhu la, mwamuna uyu, la, *Biting Of Devils*. Ndiye ine ndinaganiza kuti iyo ikanakhala nthawi, mwinamwake, yoti ndililipire, kapena kumudziwitsa iye. Ndipo mwamuna amene analemba bukhulo anali atamutsutsa mvangeri aliyense pamalopo kupatula ine, ndipo iye anali atakhala mu msonkhano wanga momwe, kotero ine ndinati, "Ine ndikuyamikira, osati kutsutsa, koma," ine ndinati, "m'baleyo, moonamtima, iye anayamikira izo pa *Christian Digest*, iye ananena kuti ine ndinali mmodzi amene sindinatengepo konse zopereka, ndi kuwapempha anthu ndalama, ndi zina zotero monga choncho, ndipo iye anayamikira izo." Ndipo mwamunayo atakhala pamenepo. Koma mwayi woti ine ndinkadziwa kuti mwamunayo anali atanena chinachake chokhudza M'bale Allen chimene sichinali cholondola.

Iye anati, "A. A. Allen analemba bukhu ili la *Biting Of Devils*."

26 Tsopano, A. A. Allen sanalembe bukhu limenelo. Ine ndinkamudziwa wolemba wa bukhu limenelo. Ndipo ine ndinati, "Tsopano, ngati mwamuna amene analemba zimenezo

sanali woonamtima mokwanira kuti apite ndi kukafufuza kuti awone amene analemba ilo asanamudzudzule M'bale Allen, ine ndikukhala ngati ndikukhulupirira kuti kutsutsa kwake kwina sikukuyenera kwa abale awa." Mukuona? Ndipo mwamunayo atakhala apo pomwe akundiyikira ine kumbuyo. Koma zinali kungomudziwitsa iye kuti chonena chake chinali cholakwika, inu mwaona, kuti M'bale Allen sanalembe konse bukhu limenelo, kulemba kwa *Biting Of Devils*.

27 Tsopano, poyankha mafunso awa, iwo ali mwa kupambana kwa kudziwa kwanga. Ndipo ngati. . .Ine ndiyesetsa kuwayankha iwo mwa Malemba.

28 Tsopano, loyamba likupezeka, ine ndikukhulupirira, mu Akorinto Woyamba, mutu wa 7 ndi ndime ya 15. Kotero tsopano ife tiyesera kupita ku Lemba limenelo ndi kukawona momwe ilo likuwonekera, ndi kuwona ngati tingamuthandize munthu wofunikira uyu amene akufunsa funsoli. Tsopano. Akorinto Woyamba, mutu wa 7, ndime ya 15. Ndipo ine ndikuganiza kuti munthuyo alipompano tsopano. Tsopano umu ndi momwe Ilo likuwerengekera:

> *Koma ngati* wosakwatirayo *achoka, muloleni iye achoke. M'bale kapena mlongo sali womangika mu* nkhani *yoteroyo*: *koma Mulungu* wa*tiyitanira ife* ku *mtendere*.

**169.** Tsopano. **Akorinto Woyamba, mutu wa 7, ndime ya 15.** Tsopano funso limene iwo anafunsa: **M'bale Branham, kodi izi zikutanthauza kuti mlongo kapena m'bale ali womasuka kuti akwatirenso?** Ayi.

29 Mwaona, inu simukumvetsa funso lake pamenepo ndi chimene iye akunena. Iwo si omasuka. Mwaona, izo zingapangitse kutsutsana mu Lemba, ndipo Malemba samadzitsutsa okha nkomwe. Mukuona? Tsopano, tiyeni. . .Inu mwaona, monga inu mukhoza kupanga Lemba (pongowerenga ndime imodzi) kunena chirichonse chimene inu mukufuna kunena, kuti chigwirizane ndi malingaliro anu. Koma inu mukuyenera kutenga lingaliro limene iwo akulankhulapo.

30 Monga ngati—ngati ine ndimayankhula kwa M'bale Neville ndipo inu—ndipo inu munandimva ine ndikunena mawu akuti, "bolodi."

31 Ndipo kenako inu nkuchokapo, inu nkukati, "Mukudziwa chimene iye amanena? Ife tinamubowa iye usikuuno." Mukuona? "Ayi," munthu winayo angati, "izo ndi zolakwika, izo zimatanthauza kuti iye—iye anali ndi ngongole ya bodi, iye amapita kukailipira iyo." Winayo nkuti, "Oh, ayi, iye samatanthauza zimenezo, iye amatanthauza bolodi m'mphepete mwa nyumba." Ndipo munthu winayo nkuti, "Ayi, ine ndikukuuzani inu chiyani, ine ndikukhulupirira iye amayesera kulankhula za kubowola bowo." Mukuona? Mukuona?

32 Iwe umayenera kufufuza zoyankhulanazo, ukatero umadziwa zomwe mukuyankhula, chifukwa Paulo apa nthawiyina akuyankha funso lawo.

33 Nthawizina iwo amati, "Baibulo limadzitsutsa Lokha." Ine ndikufuna kuti ndipeze pamenepo. Ilo silimatero. Ine ndine—ndine wa zaka sarte-thuu ndiri kuseri kwa guwa, sindinayambe ndawonapo kutsutsana panobe. Mukuona? Ilo silimadzitsutsa Lokha! Ilo limakhala chomwecho. . . Ndi inu amene mumalitsutsa Ilo, mwaona, ndipo simumalimvetsa Ilo. Mzimu Woyera ndi Wowulula, Wowulula wa Mawu. Chotero, kutsutsanako . . .

34 Mwaona, Paulo akuwalembera anthu amenewo, akuti, "Inu munafunsa chinthu *chakuti-ndi-chakuti*." Iye, kokha, iye sikuti akungonena kuti munafunsa izo, iye *akungonena* izo. Ndiye apa iye akutembenuka ndipo akuwayankha iwo, zomwe ziri zosiyana ndi zomwe iwo anafunsa.

35 Iwo anafunsa, "Ife timachita *chakuti*, ndi *chakuti*, ndi *chakuti*." Ndipo Paulo akutembenuka ndipo akunena chinachakenso, mwaona, zikuwoneka ngati zikutsutsana. Izo si choncho. Ngati mungawerenge ndime yonseyo, mutu wonsewo, inu mupeza kuti iye—iye akuyesetsa kuti afotokoze chimene iwo amulembera iye.

36 Tsopano, pomwe apa izo zimawoneka ngati izo zingapereke. . . Ndipo umo ndi momwe inu mumapezera zotsutsana mu Baibulo, koma izo siziri chomwecho. Tsopano, zikuwoneka ngati, apa, kuti munthuyo akufuna kudziwa, kapena funso la chimene iwo akufuna kudziwa:

> **Kodi m'bale kapena mlongo mwa Ambuye, akhoza kukwatira kapena kukwatiwanso ndi kukhala mfulu, ngati iwo asiyana ndi mzake kuti akakwatirenso?** Ayi.

37 Tsopano tiyeni titenge, kuyambira pa ndime ya 10:

> . . . *kwa okwatira ine ndikulamulira, komabe osati ine, koma Ambuye,* (Mukuona?)*Mkazi asachoke kwa mwamuna wake:* (Mukuona?)
>
> *Koma . . . ngati iye achoka, iye akhale wosakwatiwa, kapena ayanjanitsidwenso ndi mwamuna wake: ndipo mwamuna asamusiye mkazi wake.* (Amenewo ndi Malamulo a Ambuye, mwaona.)
>
> *Koma kwa ena onsewo ine ndikulankhula, osati Ambuye:* (Mukuona?) *Ngati m'bale aliyense ali ndi mkazi amene sakhulupirira, . . .*

38 Tsopano penyani phunziro lake, mwaona. Ndipo inu mukawerenga mpaka mmusi izi zisanachitike, kupitirira kupyola mutuwo, mupeza kuti iwo ankaganiza, "Ngati ife tinakwatira mkazi ndipo iye anali . . . ife . . . Ine ndinakwatira ndipo ndinadzakhala wokhulupirira, ndipo mkazi wanga sanali

wokhulupirira, ndiroleni ine ndimusiye iye." Oh, ayi. Si choncho izo. Inu simungachite zimenezo, Mukuona? Mwaona:

> . . .*Ngati m'bale aliyense* ali *ndi mkazi wosakhulupirira, ndipo mkaziyo akasangalatsidwa kumakhala ndi iye, mwamunayo asamusiye iye*. (Ndizo, osati chifukwa cha ukwati, ndi chifukwa cha kusakhulupirira. Osati "akwatirenso" kachiwiri. Mwaona, akhale ndi iye!)
>
> *Ndipo* ngati *mkazi amene ali ndi mwamuna wosakhulupirira,* ndi*po ngati iye asangalatsidwa kumakhala naye, mulole mkaziyo asamusiye mwamunayo*. (Ndiko kulondola! Mukuona?)
>
> *Pakuti mwamuna wosakhulupirira amayeretsedwa ndi mkazi, ndipo mkazi wosakhulupirira amayeretsedwa ndi mwamuna: ngati ana anu anali odetsedwa; koma tsopano iwo ndi oyera.*
>
> *Koma ngati wosakhulupirirayo achoka, msiyeni iye achoke.*

39 Tsopano, ngati wosakhulupirira anena kuti, "Ine sindikhala ndi iwe mopitiriranso, iwe wakhala Mkhristu." Kwa . . . Mwamuna kumuuza mkazi wake, "Chifukwa iwe wapulumutsidwa, ndipo ukutuluka mdziko kumene ife tinaliko nthawi ina, ine ndikusiya iwe." Tsopano, palibe chimene iwe ungachite pa zimenezo, muloleni iye achoke. Mukuona?

40 Kapena mkazi kunena kwa mwamuna wake, "Ine sindikasakanizikana ndi gulu ilo la oyera odzigudubuza. Ine sindichita izi! Ine ndidzilekanitsa ndipo ndikusiya iwe." Inu musasiye mpingo, inu mumulole iye achoke. Mukuona?

41 M'bale kapena mlongo samakhala womangika mu nkhani yoteroyo, ndiko kuti, ngati mzako akukusiya iwe ndipo akufuna akuchokere chifukwa cha Iwo. Iwe sumasowa kuti ungomukangamira iye. Ngati iwo akufuna kukusiyani inu ndipo iwo akufuna kukusiyani inu chifukwa cha Khristu, asiyeni iwo achoke. Koma iwe sungakwatirenso! "Koma Mulungu watiyitanira ife ku mtendere." Mukuona? Tsopano, osati kuti mukhoza kukwatiranso, iye wanena kale zimenezo, koma simuyenera kumakhala ndi mwamuna wosakhulupirira kapena mkazi wosakhulupirira ngati iye sakufuna.

42 Ngati iwo akufuna, tinene kuti "Tsopano, inu muzipitabe ku tchalitchi, ngati inu mukufuna kuti muzipita kumusi kumeneko, imeneyo ndi ntchito yanu. Iwe ukufuna kumapita ku tchalitchi chako, iwe kazipita. Kwa ine, ine sindikuwakhulupirira Iwo. Ndipo ine—ine ndizikuchitira iwe chirichonse, ine sindimaima panjira yako, iwe kazipitirira," ndiye iwe ungokhala pamenepo, posadziwa kuti moyo wanu woyeretsedwawo udzamuyeretsa wosakhulupirira ameneyo, kuwapangitsa iwo kukhulupirira.

Mukuona? Mbali iliyonse, mwamuna kapena mkazi, mwaona. Inu. . .

43 Koma tsopano kungonena kuti, "Ine, M'bale Branham, ine ndinakwatira ndipo mkazi wanga ndi wosakhulupirira, ndipo apa pali mlongo pano amene ndikhoza kumukwatira. Ndimusiya uyu ndi kumukwatira ameneyo." Oh, ayi! Ayi, ndithudi! Lumbiriro lanu liri mpaka imfa idzakulekanitseni inu, ndipo palibe china chirichonse padziko lapansi chimene chidzakulolezeni inu kuti mukwatire mu Baibulo, mpaka mzanuyo atamwalira. Uko nkulondola. Malo okhawo, palibe kukwatiranso kwina kulikonse nkomwe, pokhapokha mzanu atafa. Ndizo zonse. Mukuona?

44 Inu simungawapangitse Iwo kuti adzitsutse Okha. Kotero mungowerenga ndime za mmbuyozo ndi mtsogolo, ndipo mudzamvetsa ndiye chimene iye akunena. Tsopano, izi zikutanthauza apa, osati. . .Mukuona:

**Kodi izi zikutanthauza kuti mlongo kapena m'bale ali ndi ufulu wokwatiranso?**

45 Ayi, bwana. Mwaona, iye anafotokoza zimenezo poyamba. Onani:

> *. . .kwa okwatira ine ndikuwalamulira, komabe osati ine, koma Ambuye, Musalole kuti mkazi achoke kwa mwamuna wake:*
>
> *Koma ndipo ngati iye achoka, mulole iye akhale wosakwatiwa, kapena ayanjanitsidwenso ndi mwamuna wake:. . .*(Mukuona?)

46 Palibe zinthu zoterozo kuti wokhulupirira aliyense angayanjanitsidwenso kuti akwatirenso, ali ndi mzake wamoyo.

Tsopano, apa pali lina. Lachiwiri liri chomwechi:

**170. Kodi oyipa adzakhala ndi thupi lotani pa chiukitsiro chotsiriza pa Mpandowachifumu Waukulu Woyera Wachiweruzo?**

47 Wochimwa ameneyo adzauka mu chiukitsiro kuti adzaweruzidwe mu thupi limene iye anachitiramo tchimolo. Mukuona? Iye adzayenera kuti adzayime pa Chiweruzo mu chiwukitsiro.

48 *Chiukitsiro* si kusinthanitsa, ndi "kubweretsa icho chimene chinapita pansi." Pamene Yesu anauka kwa akufa, Iye anali thupi lomwelo limene linapita pansi, Iye anawuka mu thupi la mtundu womwewo. Ife timauka mu thupi lomwelo limene ife tinapita nalo pansi; ndi chiukitsiro, osati kusinthanitsa.

49 Tsopano, Baibulo limanena kuti, kuti ife tidzaweruzidwa molingana ndi machimo ochitidwa m'thupi. Ndipo, pamene oyipa adzauka, iye adzaweruzidwa mu thupi lomwelo limene iye anachimwiramo, chinthu chomwecho.

**171. "Adamu anamudziwa mkazi wake Eva; ndipo"** mlumikizi **"iye anaima, ndipo anabala Kaini." Ine ndimakhulupirira zonse zimene inu mumaphunzitsa, koma kodi ine ndinga—ndingamuyankhe bwanji winawake amene—amene amanena kuti iye sanatenge pakati Adamu atamudziwa iye, chifukwa cha mlumikizi *ndi*? "Adamu anamudziwa mkazi wake; ndipo iye anaima, ndipo anabala Kaini."**

50 Tsopano, ife akuluakulu tikudziwa chimene *kumudziwa* kumatanthauza. Tsopano, funso ndi lokhudza mlumikizi. Tsopano, ngati mungayang'ane, abwenzi, mwaona, inu—inu simungathe kungolipangitsa Baibulo kunena chinthu chimodzi pa malo amodzi ndi chinachake chinachakenso. Ilo likuyenera kumanena chinthu chomwecho nthawi zonse. Ndipo ngati inu muli nalo Ilo likunena chinthu chimodzi apa ndi chinachakenso apa, ndiye kutanthauzira kwanu ndi kolakwika. Mukuona? Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Inu simungakhoze kumupeza Eva atanyengedwa ndi serpenti ndipo kenako nkumupeza iye penapakenso atanyengedwa kachiwiri. Mukuona? Ndipo nthawi yoyamba imene iye ananyengedwa ndi pamene iye anatenga pakati. Inu simungamupangitse iye kuti anyengedwe kawiri.

51 Ingondirolani ine ndikuwonetseni inu pa alumikizi anuwo. Powerenga Baibulo mukuyenera kudziwa kumene alumikizi anu akupita. *Mlumikizi* ndi kumangiriza chiganizo chanu pamodzi. Mukuona? Tsopano penyani ichi. Tsopano, mu Genesis 1:26, penyani mlumikizi uyu, ndipo kenako inu mufotokoze izi ndipo kenako ine ndikuuzani momwe iye. . .pamene Adamu anamudziwa mkazi wake. Genesis, mutu wa 1, ndipo kuyambira ndime ya 26. Tsopano, mvetserani mwatcheru. Mulungu wapanga chirengedwe Chake tsopano, ndipo Mulungu analola dziko lapansi libale zinthu zokwawa ndi zinthu zonse zimene dziko lapansi linabala. Tsopano, mu mutu wa 26. . .Ndime ya 26 ya mutu wa 1 wa Genesis:

> *Ndipo Mulungu anati, Tiyeni tipange munthu mu chifaniziro chathu* chomwe*, monga mwa athu* omwe*—mawonekedwe:. . .aloleni iwo* (munthu). . . (osati *iye*; "iwo," mwaona, ambiri) *akhale ndi ulamuliro pa* nsomba *za m'nyanja, ndi pa* mbalame *za m'mlengalenga, ndi pa ng'ombe, ndi pa*. . .(Mwaona ma "ndi, ndi, ndi" akumangiriza pamodzi?). . .pa *dziko lapansi, ndi pa chinthu chokwawa chirichonse chimene chimakwawa pa dziko lapansi.*
>
> *Kotero Mulungu analenga munthu mu chifaniziro chake chomwe, mu chifaniziro cha Mulungu anamulenga iye; mwamuna ndi mkazi iye anawalenga* iwo (onse awiri mwamuna ndi mkazi).
>
> *Ndipo Mulungu anawadalitsa iwo* (pambuyo pa chirengedwe Chake, ndiye), *ndipo. . .anati kwa iwo,*

> *Mubalane, ndipo* (ndipo) *muchulukane, ndi kulidzadza dziko lapansi, ndi kuligonjetsa ilo:. . .*

52 Mlumikizi pambuyo pa mlumikizi wa chimene. . .Munthu akuyenera kuchulukana. *Ndipo*, atatha kuchulukana, kenako aligonjetse dziko lapansi; izo ndi mpaka mu Zakachikwi. Mukuona? Chabwino, "Kuligonjetsa dziko lapansi." Chabwino:

> *. . .ndi kukhala ndi ulamuliro pa* nsomba *za m'nyanja, ndi*. . .mbalame *za mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zimene zimayenda pa dziko lapansi.*

53 Tsopano, Mulungu analenga munthu mu chifaniziro Chake Chomwe, anamulenga, anawalola iwo, munthuyo, akhale ndi ulamuliro pa dziko lonse lapansi, aligonjetse ilo ndi chirichonse, ndipo anawalola iwo achite ichi ndikukhala ndi ulamuliro pa nsomba za. . .ndi chirichonse chimene Iye anachita. Ndipo kenako ife tikupeza kuti, mu Genesis 2:7. . .Mvetserani izi. Mulungu atatha kupanga dziko lapansi, atalenga munthu, atamupatsa iye ulamuliro pa dziko lapansi, atamupatsa iye chirichonse chimene iye ali nacho, ndipo Mulungu anawalenga iwo, anawauza iwo kuti achulu-. . .kuti achulukane ndi kulidzadza dziko lapansi, ndi zinthu zonsezi, ndipo zitadutsa ndime seveni za zinthu zimene Iye anali atazimalizitsa, ndi miyamba ndi dziko lapansi ndi chirichonse, "*Ndipo* Ambuye Mulungu anamuwumba munthu kuchokera ku fumbi la mnthaka." "Ndipo!" Apa Iye ali ("ndi" *mlumikizi*) akumupanga munthu amene Iye anamupanga kale. Mukuona? Kumupanga munthu:

> *Ndipo*(akumangiriza chiganizo Chake pamodzi)*Mulungu anaumba munthu* kuchokera *ku fumbi la mnthaka, ndipo anapumira* (mpweya) *mu mphuno mwake mpweya wa moyo; ndipo munthu anadzakhala solo yamoyo*.

54 Tsopano, taganizani za zimenezo! Iye atatha kumupanga munthu, akazi ndi amuna, mu Genesis 1:26 mpaka 28, Iye anamupanga munthu mu chifaniziro Chake Chomwe, anamulenga iye ndipo anamupatsa iye, agonjetse ma ufumu, ndipo anamupatsa iye mphamvu zonse izi ndi chirichonse, ndipo komabe Iye anali asanamulengebe munthu.

55 Mwaona, Satana anali atamunyenga kale Eva. Zoona, Adamu anamudziwa iye, koma iye anali atanyengedwa kale. Chifukwa kumbuyo komwe kuno iye. . .pamene iwo. . .iwo asanabwere. . .Pamene iwo anabwera mu chiweruzo, Iye anati. . .Ndipo Mulungu anawasonkhanitsa iwo pamodzi ndipo anati, "Ndani wachita ichi?" Anawafunsa iwo funsolo.

Adamu anati, "Mkazi amene Inu munandipatsa ine."

Ndipo mkaziyo anati, "Serpenti anandinyenga ine."

56 Ndipo Mulungu anayika themberero pa iwo, ndi chirichonse monga chomwecho. Ndipo *kenako* Adamu anamudziwa mkazi wake, mwaona, iye atatha kunyengedwa kale ndikukhala mayi. Basi chimodzimodzi monga Mulungu anamupangira munthu mmbuyo umu mu Genesis 1:26 ndipo komabe iye anali asanapangidwebe. Mukuona? Chabwino.

57 Tsopano penyani, tiyeni titsike pansi apa ndipo tikawerenge, nafenso:

> *Ndipo Adamu anamutcha* mkazi *wake*. . .*Eva; chifukwa iye anali mayi wa* zinthu *zonse zamoyo,* zonse. . .kapena *mayi wa zamoyo zonse.* Anamutcha mkazi wake. . .anamutcha mkaziyo mkazake chifukwa iye anali. . .kapena mkazi chifukwa iye anali. . .wa zamoyo zonse.
>
> Ndipo *kwa Adamu nayenso ndi kwa mkazi wake* A*MBUYE*. . .*anapanga zovala za* chikopa kuti ziwaphimbe *iwo*.

58 Tsopano, tsopano zindikirani mu Genesis kenanso, 1:21, Mulungu analenga zinsomba mnyanja. Iye anachita chirichonse, ndipo anapanga chirengedwe, anamupanga munthu mu chifanizo Chake Chomwe. Anamupanga munthu, osati "ka" munthu, munthu wathunthu, onse a iwo mu chifaniziro Chake Chomwe. Mukuona? Ndipo mu chifaniziro cha Mulungu Iye anawalenga iwo; mwamuna ndi mkazi, anamulenga iye awiri onse monga chomwecho.

59 Ndipo tsopano ife tikupeza, cha apa kachiwiri, Iye atatha kumupanga munthu mu chifaniziro Chake Chomwe, Iye atatha kumulenga iye cha kuno mwamuna ndi mkazi, apa Iye akumupanga munthu kuchokera ku fumbi la dziko lapansi.

60 Ndiyeno, Iye atatha kuchita zimenezo, Iye atatha kumupanga iye mwamuna ndi mkazi, kenako Iye akubwereranso kuno ndi kudzamupangira iye mkazi, Iye atamupanga kale iye. Mukuona?

61 Mwaona, mlumikizi wanu akumangiriza chiganizo chimenecho pamodzi. Chimodzimodzi basi monga zinanenera, tsopano, *apa*, "Mulungu anamulenga munthu mu chifaniziro Chake Chomwe, mwa mawonekedwe Ake Iye anamulenga iye," ndi Mulungu akuyankhula mmaganizo Ake, mmalingaliro Ake, chimene Iye anali nacho. *Apa* ndi pamene Iye anachita kwenikweni chinthucho.

62 Yesu anali Mwanawankhosa wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi; Iye sanaphedwe kwa zaka foro sauzande pambuyo pake. Mukuona?

63 Chotero serpenti anamunyenga Eva. Ndizo moonadi. Kenako chiweruzo chitachitika, ndiye Adamu anamudziwa mkazi wake. Ndipo kenako iye anaima ndipo anabala mwana

wamwamuna, Kaini. Inu mukumvetsa zimenezo? Mwaona, mlumikiziyo akungopitirira pa zomwe Adamu anachita, osati zomwe zinachitidwa Adamu asanakhalepo.

64 Ndipo taonani apa, ngati inu mukufuna kuti muchite zimenezo, mu neno lalikulu limenelo apa, ine ndikukhulupirira ife tikulipeza ilo apa mu. . .ndipo apa mu mutu wa 4, ine ndikukhulupirira ndi pamenepo.

> *Ndipo Adamu anamudziwa. . .mkazi wake; ndipo iye anaima, ndipo anabala Kaini, ndipo* (mlumikizi) *anati, ine ndalandira munthu kuchokera kwa* A*MBUYE*.

65 Ndiye kwenikweni sanali Adamu, anali mwana wa Mulungu mwa iye. Mukuona? Mukuona? Ngati inu mukufuna kuti muyike mlumikizi wanu pamenepo, mwaona ("ndipo" kachiwiri), "Ndapeza munthu kuchokera kwa Mulungu." Ndiye kunena kuti Mulungu anamupatsa iye chinthu chosalidwa chija chotchedwa Kaini. Kodi gwero la zonyansa zonsezo ndi nyansi ndi zinthu zimene Kaini anali nazo, limachokera kwa Mulungu? Sizikanakhala chomwecho! Mukuona? Iye ananyengedwa ndi serpenti, ndipo serpenti. . .iye anali atakhala kale mayi. Kenako Adamu anamudziwa iye, ndithudi iye anatero, iye anapita ndipo anakakhala ndi iye ngati mkazi wake, koma iye anali woti akhala mayi wa mwana uyu.

66 Ndipo kenako pamene mwana wa Adamu potsiriza anadzabadwa, iye anali wodekha, wokoma, wodzichepetsa, munthu wofatsa monga Adamu.

67 Koma munthu uyu, kodi kunama kwathunthu kumeneko, kodi tchimo limenelo linachokera kuti? Kodi munthu uyu, Kaini, wakupha uja? Ndipo Baibulo linanena kuti "Mdierekezi ndi wakupha." Kodi bodza limenelo linachokera kuti? (Mdierekezi ndi atate wa bodza; iye ndi wabodza ndipo atate wa bodza.) Izo zinkayenera kubwera kuchokera ku gwero lina kunja kwa Mulungu. Chotero Kaini anali woipayo, ndipo atate ake anali Satana; ndipo anabweretsapo woyipa uyu.

Ndipo kenako, ndithudi, Adamu anamudziwa mkazi wake, ndithudi.

68 Ndipo, eya, mwinamwake ngati inu mukananena monga chonchi. Ine ndikhoza kunena, kudzitenga ndekha, chabwino, tsopano, Rabekah anabadwa, ndipo patapita kanthawi panadzabwera motsatira. . .

69 Ndinali kuwerenga tsiku lina nkhani ya Yosefe, ndipo ndinakondowezedwa kwambiri ndi nkhani ya Yosefe. Ine ndinalowa mu kachipinda kakang'ono ndipo ndinagwada pansi, kumtunda uko mu Minneapolis, ndipo ine ndinati, "Ambuye Mulungu, momwe ine ndikukuthokozerani Inu chifukwa cha munthu ngati Yosefe!" Ndipo ndinaganiza, "Ngati ine ine. . . Ndikanakonda ndikanamutcha Billy Paul, 'Joseph,' chifukwa cha khalidwe lolemekezeka kwambiri limenelo." Palibe chilema

chimodzi chomutsutsa iye paliponse mu Baibulo, woimira wangwiro wa Khristu mu njira iliyonse. Ndinaganiza, "Momwe ndikanakondera . . ." Ine ndinati, "Oh, ngati nditakhala ndi mnyamata, ine ndingamutche iye 'Joseph.'"

70 Ndipo basi pomwepo Kuwala kuja kunabwera kukuyenda kulowa mnyumbamo ndipo kunati, "Iwe udzakhala ndi mwana wamwamuna ndipo udzamutcha dzina lake 'Joseph.'"

71 Ine ndinamudziwa mkazi wanga, ndithudi, iye anabala Sarah. Kenako ndinadzamudziwa mkazi wanga *ndipo* anadzabala Joseph. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Mwaona, izo zinalibe chochita ndi woyambayo. Lonjezo la Mulungu linali "Joseph," Sarah anadzabwera pakati pa zimenezo. Osati kumuyika Sarah mu chochitika cha mtundu umenewo, koma kuti ndingokuwonetsani inu chimene ine—chimene ine ndikutanthauza. Mwaona, izo . . . Sarah anali wotumizidwa ndi Mulungu, nayenso. Ndipo kotero ndiye ife tikudziwa zimenezo.

72 Tsopano, koma, mwaona. Mulungu, pamene Iye anapereka chiweruzo kwa Adamu ndi Eva, iye anali atachita kale tchimolo Iye asanapereke chiweruzo. Ndipo, mvetserani, kodi inu munayamba mwadziwa kuti mwana woyamba amene anayamba wabadwapo mu dziko anali "wobadwa mu tchimo, wowumbidwa mu kusaeruzika, anabwera ku dziko akunena mabodza"? Woyamba yemwe amene anayamba wabadwa anabadwa mwanjira imeneyo, chifukwa . . .

73 Inu mukuti, "Nanga bwanji Adamu ndi Eva?" Iwo sanabadwe. Iwo analengedwa. Mukuona?

74 Koma mwana woyamba amene anayamba wabwera anabadwa mu tchimo, kotero izo zikuyenera kukhala mzere umenewo. "Munthu wobadwa mwa mkazi ndi wa masiku owerengeka ndi odzadza ndi mavuto." Iye amabadwira mu tchimo. Ndi chifukwa chake iye akuyenera kuti abadwe kachiwiri, mwaona, mwa Mzimu; osati mwa *lingaliro* lauzimu; mwa Kubadwa kwauzimu, mwaona, izo zimamusintha iye, zimamupanga iye kukhala cholengedwa chatsopano. Munthu woyamba amene anabadwa anababwa mu tchimo.

75 Ndiye, pankayenera kukhala Mmodzi wobwera popanda kugonana. Tsopano, ngati kugonana sichinali chinthu choyambirira, ndiye nchifukwa chiyani iwo ankayenera kukhala ndi Mmodzi mu kugonana kuti awombole mtundu wonse wa anthu? Nchifukwa chiyani Iye sanangomubweretsa mmodzi pansi mmakonde ndi kuti, "Apa pali Mmodzi wolungamayo amene *amaganiza* bwino"? Izo zinkayenera kubwera kudzera mu kugonana, kubwera kudzera mwa mkazi, chifukwa umo ndi momwe izo zinabwerera pa malo oyambirira. Kudzera mu kugonana, zinabweretsa kusalungama; ndipo kudzera mu kugonana, zinabweretsa Chirungamo. Mukuona? Mulungu,

popanda chigololo, popanda chilakolako cha kugonana, anabala Yesu Khristu mwa kukhala ndi pakati kwachiyero, pomuphimba Maria ndi kulenga mwa iye Mwana uyu; amene anabwera mwa kugonana. Ndipo, kupyolera mu zimenezo, Magazi Ake Oyera anawombola mtundu wonse wakugwa. Mukuona? Kotero izo zikuyenera kukhala, palibe njira ina ya zimenezo.

76 Munthu aliyense wobadwa mwa mkazi ndi wopita ku imfa, iye amakhala wakufa pamene iye wabadwa. Uko nkulondola.

77 Chimenecho ndi chifukwa chake ine ndimayankhula tsiku lina momwe ife tiri nacho chitsimikizo chodala chimenecho tsopano.

78 Pamene Israeli...Sichoncho izo...Ine ndimayankhula zinthu zambiri zimene ziribe kanthu kwa izo, koma nthawizina Ambuye amandipatsa ine chinachake ndipo chimangondikondoweza ine. Kotero pamene Iye anandipatsa ine icho, icho chinandikondoweza ine kuposa chirichonse chimene ine ndinakhalapo nacho mzakazi. Pamene Iye anandipatsa ine icho tsiku lina, pamene ine ndinamuwona Israeli ameneyo, kapolo, analibe kwawo, ana a Mulungu. Kuponyeramo mkate woumbidwa, chirichonse chimene iwo angafune! Oh, ngati iwo akanakhala ndi kwawo kumene akanatha kukhala mwa mtendere, kupeza zofunika pamoyo wawo ndi thukuta la zipumi zawo!

79 Ndipo, tsiku lina, akubwera kuchokera mchipululu kunabwera mneneri, akutsogoleredwa ndi Lawi la Moto, ndipo anawauza iwo za dziko lolonjezedwa. Palibe amene anakhalapo kumeneko, iwo sankadziwa kanthu za izo. Koma ilo linali lonjezo. Pa ilo iwo anamukhulupirira ndi kumutsatira mneneri uyu mpaka iwo anafika pafupi ndi dziko lolonjezedwa.

80 Kenako panali mboni yotchedwa *Yoswa*, amene amatanthauza "Yehova-mpulumutsi," anawoloka Yorodani kukalowa mdziko limenelo, ndipo anabwerera ndi umboni wakuti dziko limenelo linali ndendende basi chimene mneneri uja ananena kuti linali ndi Mawu a Mulungu. Iwo anali ndi mulu wa mipesa, zinkatengera amuna awiri kuti anyamule, ndipo iwo ankakhoza kulawa chipatso chapachiyambicho kuchokera ku dzikolo. Palibe amene ankadziwa kuti dzikolo linalipo, iwo ankangokhulupirira izo. Iwo anatuluka mwa chikhulupiriro ndipo anakhulupirira izo.

81 Tsopano pamene iwo analitenga dziko lawo, momwe iwo analiri osangalala! Aliyense ankakhoza kukhala mwa mtendere, kukhala ndi munda wake waung'ono, kukhala ndi ana ake ndi chirichonse. Koma, komabe, ukalamba potsiriza unamupeza iye, ndipo imfa inamutsekereza iye ndi kumutenga iye.

82 Kenako kutsika kuchokera ku makonde a Kumwamba, kudzera mwa mkazi, kunadza Wankhondo wina wamkulu, wamkulu wa iwo onse, Mulungu Mwiniwake akudziwonetsera

mu thupi, Yesu Khristu. Ndipo Iye anauza Israeli momwe iwo analiri anthu opambana, koma imfa inayang'anizana nawo, Iye anati, "Koma ndikukuuzani inu za dziko lina. Mu Ufumu wa Atate Anga muli nyumba zambiri. Ngati sizinali chomwecho ndikanakuuzani inu. Ndinu okondwa m'dziko lanu, muli ndi nyumba zanu, muli ndi ana anu. Koma inu mukumuyika mmanda aliyense kutsidya uko ndipo zikuwoneka ngati ndiwo mathero."

83 Yobu anaziwona izo, anati, "Ngati mtengo ukafa, iwo umadzakhalanso ndi moyo. Koma munthu amagona pansi ndi kupereka mzimu, iye ali kuti? Ana ake amabwera kudzamupatsa iye ulemu ndipo iye samazindikira izo ayi. Oh, kuti Inu mundibise ine mmanda, kundisunga ine mmalo achinsinsi mpaka mkwiyo Wanu utapita!" Iye anati, "Ngati munthu afa kodi iye adzakhalanso ndi moyo?"

84 Zaka foro sauzande izo zisanachitike, iwo ankayembekezera chinachake kupyola manda amenewo. Zinthu zazikulu zonse zimene Mulungu anawapatsa iwo, nyumba, banja ndi ana, ndi mpingo, ndi chirichonse, ndi aneneri, ndi anthu otchuka mpaka nthawi iyi, komabe aliyense anafa ndipo anapita ku manda ake. Koma apa pakubwera Mmodzi ndipo akuti, "Mu Ufumu wa Atate Anga muli nyumba zambiri, ndipo Ine ndikupita kukakukonzerani inu malo." Monga Yoswa, Iye anakumana ndi Kadeshi-barnea Wake.

85 Pamene Israeli anafika pa Kadeshi-barnea. . .Ndipo Kadeshi unali mpando wachiweruzo wa dziko lapansi pa nthawi imeneyo, akasupe seveni kuchokera ku kasupe wamkulu, kutanthauza chiweruzo, monga Nyumba ya Mulungu ndi Mipingo imene imatuluka mwa Iyo. Ndipo Yoswa, kuchokera ku Kadeshi-barnea, anawoloka kupita ku dziko lolonjezedwa kuti akabweretse umboni.

86 Tsopano, Yesu anakumana ndi *Kadeshi* Wake. Chinali chiyani icho? Mpando wachiweruzo! Iwo unali kuti? Pa Kalvare, pamene Mulungu anamuweruza Iye chifukwa cha machimo a dziko lapansi. Kodi iwo anachita chiyani? Iye anakumana ndi imfa, malipiro a Mulungu. Kuti akawayanjanitse ochimwa kwa Mulungu, Iye anafa imfa ndipo anawoloka mtsinje wa Yordani (wa imfa). Iwo anamuika mmanda Iye.

87 Iye anafa mpaka mwezi ndi nyenyezi zinachita manyazi zokha. Iye anafa mpaka dziko linali ndi kusokonezeka kwa manjenje. Ilo linagwedezeka mpaka miyala inagudubuzika kuchokera m'mapiri. Ilo linagwedezeka mpaka nyenyezi sizikanatha kuwala, mwezi sunakanatha kuwala, ndipo dzuwa linalowa pakati pa tsiku. Iye anafa! Wakufa kwambiri mpaka Wachiroma anatenga nkondo wa mapaundi teni ndi kuwuzika kwathunthu kupyoza mtima Wake; madzi ndi Magazi. Iye anali atafa! Iye anawoloka Yordani. Ndipo iwo anamuyika Iye

m'manda ndipo anagudubuzira a—mwala pa iwo, zinatengera amuna ochuluka kuti achite zimenezo. Iye anali atafa! Iwo anaika chisindikizo cha Chiroma pa iwo.

88 Koma mmawa wa Chiwukitsiro Iye anabwerera kuchokera kutsidya la Yordani, ndipo anati, "Ine ndine Iye amene ndinali wakufa; ndipo ndiri wamoyo kwa nthawizonse!"

Ena a iwo anati, "Ife tikuwona mzimu."

89 Anati, "Ndikhudzeni ine. Kodi mzimu umakhala ndi mnofu ndi mafupa monga Ine ndiriri nazo?" Anati, "Muli ndi chakudya chirichonse? Ndibweretsereni Ine chinachake." Ndipo iwo anampatsa Iye nsomba ndi mkate. Ndipo Iye anadya izo. Iye anali Munthu!

90 Kodi Iye anali chiyani? Kubweretsanso umboni wakuti kuli Dziko limene ife tikupitako. Kodi Iye anachita chiyani? Iye, monga Yoswa, Iye anabweretsa umboni wa Ilo. Iye anati, "Tsopano, ngati inu mukufuna umboni wa Ilo, 'Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo, ndipo inu mudzalandira Mzimu Woyera.' Umenewo ndiwo umboni umene unandiwukitsa Ine. Ine ndidzakupatsani inu Chikole cha cholowa chanu." Ndiyeno chinachitika ndi chiyani? Pa Tsiku la Pentekoste Mzimu Woyera unabwera pa wokhulupirira.

91 Tsopano ife timachita chiyani? Timavomereza machimo athu, kudziwerengera tokha akufa, oyikidwa ndi Iye mu ubatizo, kuukitsidwa ndi Iye mu chiukitsiro Chake. Kuti titani? "Kukhala mmalo Ammwambamwamba ndi Iye." Pamenepo ndi pamene ife tiri usikuuno, titakhala (osati mwathupi) mwauzimu, malingaliro athu, maganizo athu, miyoyo yathu zili kutali kwambiri ndi zosamalira za dziko pakali pano. Ife ndi chiyani? "Mmalo Ammwambamwamba *mwa* Khristu Yesu." Kodi ife timalowa bwanji mwa Iwo? "Mwa Mzimu umodzi," Akorinto Woyamba, mutu wa 12, "mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa ndi Mzimu Woyera kulowa mu Thupi limodzi la okhulupirira." Ufumu wachinsinsi wa Mulungu!

92 Mmenemo timayang'ana m'mbuyo ndi kuwona pamene ife tinkanama ndi kuba ndi kuchita chinyengo ndi kusuta ndi kuchita zinthu zimene zinali zolakwika. Ife tinadzuka kuchoka ku zimenezo. Ife tiri mmalo Ammwambamwamba. Icho ndi chiyani? Umboni wakuti tsiku lina tidzakhala ndi thupi ngati thupi Lake Lomwe laulemelero. Umenewo ndi umboni weniweni wa chiukitsiro, chifukwa, mwakungoyankhula, ife tinaukitsidwa kale ndi Iye, mwakungoyankhula ife tinafa kale.

93 William Branham amene ankakhala moyo sakukhala moyo panonso, iye wakhala atafa kwa zaka sarte-chakuti zosamvetsetseka, tsopano ndi cholengedwa chatsopano. Orman Neville yemwe ankakhala moyo salinso moyo, iye anafa zaka zambiri izo zisanachitike, ichi ndi cholengedwa chatsopano.

Orman Neville anafa, a—wa mpikisano wa akavalo, wanjuga, kapena chirichonse chimene iye anali, munthu yemwe poyamba anali wamoyo ndi wakufa. Ine sindikudziwa, M'bale Neville sanali zimenezo; koma chirichonse chimene icho chinali, iye ndi wolakwa pa izo zonse, "Wolakwira chaching'ono ndi wolakwira zonse." Chirichonse chimene inu munali, ndinu wochimwa, ndi chimene inu muli.

94 Ndipo ndinu akufa chifukwa mumakonda zinthu za mdziko lapansi. Ndipo bola ngati mukulikondabe dziko lapansi, ziribe kanthu momwe mungavomerezere kukhala pamwamba *apa*, inu simuli pamwamba apa, inu muli kumusi *uko* apobe. "Iye amene akonda dziko lapansi kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichinamulowebe iye."

95 Koma pamene inu mukwera pamwamba pa zimenezo ku zinthu Zakumwamba ndiye mukhazikitse zokonda zanu pa zinthu zakumwamba, chifukwa inu munaukitsidwa ndi Khristu ndipo tsopano mukukhala limodzi m'malo Ammwambamwamba. Mungokhala otsimikizika, palibe chinthu chimene chingakupwetekeni inu, palibe chinthu. Ngakhale imfa iyoeni ilibe. . .siyingachite kanthu kwa inu. Inu munazikika kale mwa Khristu. Chitsimikizo, Chikole, kulipira kochepa kwabweretsedwa kale, inu mwalandira Icho. Kodi inu munachita chiyani? Munawuka limodzi ndi Iye mu chiwukitsiro.

96 Yang'anani mmbuyo kumene ine ndinali. Tsopano ine ndiri pamwamba pa zimenezo. Chifukwa chiyani? Mwa chisomo Chake Iye anandikweza mmwamba, ndipo apa ine ndakhala mmalo ammwambamwamba mwa Khristu. Oh, mai! Ndi zimenezotu pamenepo. Kenako Baibulo limakhala Bukhu latsopano. Ndiye inu mumaliwerenga Ilo kudzera mmaso auzimu ndi kumvetsa kwauzimu. Zikatero umawona maina ndi amlowammalo, ndipo kenako umawona mphambano. . .ndi alumikizi, ine ndikutanthauza, ndi zina zotero, mu Baibulo.

97 Oh, pamene Ilo likuti. . .Iwo amati, "Ilo limadzitsutsa Lokha"; inu mukuwerengera pansi *apa*. Fikani pamwamba *apa* ndipo muwerenge Ilo, Ilo lonse lidzakhala losiyana ndiye. Inu mukuona? Uko nkulondola. Ndithudi. Ndithudi, Ilo limatanthauza chinthu chonse chatsopano pamene muliwerenga Ilo mu Mzimu. Inde.

Funso lina ili si funso kwenikweni, ilo likungoti:

**172. Ine ndinakhala zaka zambiri mu tchimo kufikira nditawapeza Ambuye. Chonde, M'bale Branham, ine ndachimwa kachiwiri ndipo ine sindiri woyenera kubwera pamaso panu mmalo oyera awa. Chonde ndiuzeni ngati ndingathe kubwezeretsedwanso kwathunthu. Chonde ndithandizeni ine, M'bale Branham, ine ndiri ndi mdierekezi mwa ine. Ndithandizeni ine! Kodi inu**

**mungayike manja anu pa ine ndi kundibwezeretsa ine kachiwiri?**

98 Tsopano, apo pali funso, ine sindinalizindikire ilo pamene ine ndimawerenga ilo kanthawi kapitako. Apo pali funso. Tsopano, ngati munthu ameneyo alipompano. . .Ndiroleni ine ndingoliwerenga ilo kwa inu:

> **Ine ndakhala—ndakhala zaka zambiri mu tchimo mpaka ndinawapeza Ambuye. Chonde, M'bale Branham. . .** (Mukuona?)**. . .Ine ndachimwa kachiwiri ndipo sindine woyenera kubwera pamaso panu m'malo oyera awa. Chonde ndiwuzeni ngati ndingabwezeretsedwe kwathunthu kachiwiri.**

99 Inde! Iwe sunachimwe, mzanga, motalikira kwambiri mwa Mulungu kuti sungakhoze kubwezeretsedwa. Ngati ukanachimwa motalikira kwambiri kuti iwe sungathe kubwezeretsedwa, iwe sukana*funa* kuti ubwezeretsedwe. Mukuona? Mukuona? Koma bola ngati pali Chinachake chikuchita ndi mtima wako, iwe ukadali pamzere wobwezeretsedwa.

100 "Kulakwira chaching'ono ndi kulakwira zonse." Ine ndachimwapo nthawi zambiri, tsiku lirilonse aliyense wa ife timachita zinthu zimene sitimafuna kuzichita.

101 Izo zimakhala mu mtima mwathu. . .Iwe sumafuna kuti ukhale chomwecho kapena iwe sibwenzi utafunsa funso ili. Mukuona? Chimenecho pachokha ndi chitsimikizo chakuti Mulungu akuchitabe ndi iwe. Mwinamwake iwe wachita manjenje, mwinamwake Satana akukuuza kuti sungathe kubwezeretsedwa. Iye akunama, ndithudi, iye akutero. Chifukwa, penyani, ngati pali kuya, kukuyitana, pakuyenera kukhala Kuya kuti kuyankhire ku kuyitanako. Ngati pali njala ya Chinachake, Chinachakecho chikuyenera kukhala kwinakwake kapena iwe sibwenzi uli ndi njala ya Icho. Mukuona?

102 Monga ndanenera nthawi zambiri. Nsomba isanakhale ndi chipsyepsye pa nsana pake, pankayenera kuti pakhale madzi poyamba kuti iyo izisambiramo kapena iyo sikanakhala ndi chipsyepsye chirichonse. Pasanakhale mtengo woti umere mu nthaka, pankayenera kukhala nthaka poyamba mtengowo usanakhalepo, chifukwa nthaka inkayenera kukhalapo poyamba kuti mtengowo udzamerepo.

103 Tsopano, pasanakhale chirengedwe, pakuyenera kukhala pali Mlengi kuti adzalenge chirengedwecho. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Tsopano, bola ngati ukufuna ndi kuchita njala yobwerera kwa Mulungu, pali Mulungu penapake akuyitanira kwa iwe, mwaona, kapena iwe sibwenzi ukumva njalayo. Alipo Mlengi!

104 Tsopano, ngati iwe. . .Alipo malo amene iwe ukhoza kuwolokera komwe sungathe kubwererakonso, koma pamene izo ziri kuti iuwe uli kumusi uko kachiwiri muchikhalidwe chomwecho chimene iwe unalimo. Izo zikungosonyeza kuti iwe *unangogwa* ku chisomo. Kubwerera m'mbuyo si *kutayika*. Ine ndikufuna winawake andiuze ine pamene kubwerera mmbuyo kuli *kutayika*, ndipo atsimikizire zimenezo kwa Baibulo. Wobwerera mmbuyo sanatayike, iye wangochoka mu chiyanjano.

105 Israeli anabwerera mmbuyo koma sanataye pangano lawo, iwo anataya awo—matamando awo ndi chimwemwe.

106 Davide anataya chimwemwe cha chipulumutso chake pamene anamutenga Bathsheba, mkazi wa Uriya, koma sanataye chipulumutso chake. Iye sananene kuti, "Mubwezeretse kwa ine chipulumutso changa." Anati, "Mubwezeretse kwa ine *chimwemwe* cha chipulumutso changa."

107 Oh, pali zambiri zamalamulo izi lero, za "musakhudze, musalawe." Iwe sumachita zinthu mwalamulo.

108 Ine sindinabwere ku mpingo kuno usikuuno mwalamulo. Ndikumverera kutopa, ine—ine—ine ndakhala ndiri wamanjenje, ndasokonezeka, ndikudabwa za chinachake chimene chiri patsogolo panga, mtima wanga ukutentha, ngakhale motero mochuluka mpaka mtima wanga ukugunda mofooka. Ndiri ndi dzanzi, kupweteka, pa miniti yomwe ino, kumangowombera mmbuyo ndi mtsogolo, chokwera ndi chotsika kudutsa *apa*. Wofooka, wamanjenje, ndikunjenjemera; kugwira *apa* ndi kufinya; zala zanga zakuphazi ndazifinyira mu nsapato zanga. Ndinamverera kalikonse koma kubwera kumusi kuno. Ndabwera chifukwa chiyani, ndiye? Chifukwa ndimamukonda Mulungu. Kukhala moyo kapena kufa, ine ndikuyenera kuyima pano chifukwa cha Iye. Si chifukwa chakuti ndikuyenera kutero. Iye sakanasamala ngati ine ndikanatero kapena ayi. Ine ndikana. . .Ngati ine ndikanafa ine ndikanapita Kumwamba, mulimonse. Koma ine ndikubwera chifukwa ine ndimamukonda Iye. Iwe umamutumikira Mulungu chifukwa chakuti umamukonda Iye, osati chifukwa chakuti ukungoyenera kuchita zimenezo. Chifukwa umamukonda Iye mokwanira!

109 Sindine woona kwa mkazi wanga chifukwa ndimawopa kuti angandisiye. Ndine woona kwa iye chifukwa ndimamukonda iye. Palibe mkazi wina padziko lapansi koma iye. Chimenecho ndi chifukwa chimene ine ndiri woona kwa iye. Osati chifukwa. . . Ngati nditalakwitsa ndipo iwo nkuganiza kuti ndachita chinachake cholakwika, nkubwera kwa iye, ndikuti, "Meda, wokondedwa, ine sindimatanthauza kuti ndichite zimenezo." Iye angakhoze kundikhululukira ine chifukwa cha izo, ndikudziwa kuti iye angatero. Ine ndingamukhululukire iye; ine ndimamukonda iye. Koma ine—ine ndingamukhululukire iye; iye

angandikhulululukire ine. Koma sindingachite zimenezo pachabe, ine ndimamukonda iye kwambiri kuti ndichite zimenezo. Sichifukwa chakuti sindimaganiza kuti iye angandikhulululukire ine, ndi lingaliro lakuti ndimamukonda iye kwambiri kuti ndichite izo kuyamba ndi kuyamba. Ndipo malingana ngati ine ndikumukonda iye monga choncho, ine sindidzachita konse zimenezo; ndipo ngati iye amandikonda momwe amayenera kuchitira, iye sadzateronso.

110 Ndipo ngati inu mumawakonda Ambuye ndi mtima wanu wonse, inu simukusowa kuti muzidandaula za zinthu izi. Ngati mwalakwitsa, inu simumachimwa mwadala, inu mwangochita chinachake cholakwika. Mwaona, mwabwerera mmbuyo. Zoona, inu munali pamwamba apa mu chiyanjano, inu mwagwera pansi mmatope awa pansi apa kachiwiri.

111 Koma ndi chiyani chimenecho? Izo ziri ngati a—mphungu. Nthawi ina ine ndinawona, kuno ku Cincinnati Zoo, ine ndinamutenga Sarah ndipo tinkapita kumusi kumeneko... Ngati pali chirichonse chimene ine ndinachiwonapo chimene chimandipweteka ine, ndi kuwona chinachake chiri mu khola.

112 Ine sindingathe kupirira basi kuwona chirichonse chiri mu khola, ngakhale mbalame zazing'ono. Ndipo ine ndikudziwa akazi inu muli nazo mbalame zazing'ono zimenezo, inu muzitulutse izo.

113 Pamene ndinali mnyamata wamng'ono ine ndinkati, "Ngati ndikadzapeza mpata, pamene ndidzafike pokhala mwamuna, ndizidzazembera m'nyumba iliyonse ndi kukamasula tinthu tating'ono tosauka timeneto." Inde, bwana. Ine ndinati... Zitakhala kuntunda uko padzuwa lotentha, ndipo izo zikuti, "Hah, hah, hah," ndipo mkazi kunja kwinakwake pa khonde la kumbuyo akusuta ndudu, ndipo mbalame yaying'ono yosaukayo itakhala pamenepo ikupsya. Iyo siyingachite kalikonse za izo, iyo imangoyenera kukhala pamenepo. Ndipo iyo sinabadwire zimenezo! Ine ndinaganiza, "Mnyamata, ngati ndingazembere pamenepo ndi kukaitulutsa iyo, iyo siyingakhale pamenepo nthawi yotalika kwambiri." Mukuona?

114 Ine ndimadana nazo kuwona chirichonse chiri mu khola. Ine ndimadana ndi kumuwona munthu akudzitcha yekha *Mkhristu* ndiye atayikidwa mu khola ndi mtundu wina wa kachikhulupiriro ka mpingo, "Ine sindingathe kunena, 'Ameni.' Ine—ine sindingakhulupirire mu *Izo*. Abusa amati, 'Musakhulupirire Zimenezo.'" Oh, mai, kalanga! Inu munabadwa mfulu.

115 Ndiye nanga bwanji mphungu yayikulu? Iyo ndi mbalame ya mmwamba. Iyo imakhala kutali pamwamba pa mitambo. Uko ndi kumene iyo imapita m'mawa. Mmwamba kwambiri, palibe china chirichonse chimene chingayitsatire iyo! Osati mbalame

ina . . . iyo ingasweke mlengalenga ngati ingayesere kutsatira iyo. Iyo ndi mbalame yopangidwa mwapadera.

116 Ndiyeno winawake anaigwira iyo mu msampha wopangidwa ndi anthu, iye anayigwira mphungu yaikulu iyi ndi kudzaiyika iyo mu khola ili. Ndipo chinthu chosauka chokalambacho . . . Ndinayang'ana pa iyo ndipo mtima wanga unangotentha. Iyo inayang'ana mbali imeneyo monga *choncho* ndipo sinkadziwa momwe ikanatulukira mu khola limenelo. Iyo imangokhoza kudutsa pamenepo, ndipo iyo—iyo inkadziwa momwe ikanaulukira, ndipo iyo inkayamba kukupiza mapiko ake. Ndipo apa iyo inkapita, iyo inkamenyetsa mutu wake pa zitsulo ndi kumenyetsa nthenga kuchokera mu nkono wake, nthenga za mmapiko apa, ndi pa mutu pake ponse, mpaka iyo inali ikuwukha magazi. Iyo inkamenya chitsulocho mwamphamvu kwambiri moti chinkaigwetsera iyo chagada pa nsana wake. Ndipo iyo inkagona pamenepo ndi kutembenuza maso owoneka-otopa amenewo, kuyang'ana mmwamba kuloza mumlengalenga, "Uko ndi komwe kuli kwathu. Uko ndiko kwathu. Kumeneko ndi kumene ine ndinabadwira. Koma, penyani, pakati pa ine ndi kumeneko pali khola. Chabwino, chinthu chokhacho chimene ine ndikuchidziwa, ndingoyika malingaliro anga kwa icho ndipo apa ndikubwera," ndipo "nkudzazimenyetsa," iyo inkapitanso mmbuyo kachiwiri.

117 Ine ndinaganiza, "Oh, mai, kodi zimenezo si zoipa! Ndinkakhumba iwo akanaigulitsa iyo kwa ine. Ine ndikanapinyolitsa Ford yanga kuti ndigule iyo, mwaona, kuti ndingoyimasula iyo." Mukuona? Oh, izo zinkandipangitsa ine kumverera moyipa kwambiri, mbalame yayikulu yosauka imeneyo pamenepo, ikumenyetsa nthenga . . . Ndinaganiza, "Amenewo ndi mawonekedwe oyipa kwambiri amene ndinawawonapo."

118 Ayi, ine ndibweze zimenezo, mawonekedwe oyipa kwambiri amene ine ndinawawonapo ndi munthu wobadwa kuti akhale mwana wa Mulungu ndipo kenako nkumangidwa mu kachikhulupiriro kenakake. Ndipo iye amayang'ana mmwamba umo ndi kumuwona Mulungu amene iye akufuna kwenikweni kuti amutumikire, koma iye sangathe kuchita zimenezo. Iwo sangamulole iye kuti achite zimenezo, mwaona, wayikidwa mu khola. Icho ndi chinthu choyipa.

119 Inde, inde, mlongo, m'bale, aliyense amene analemba izi, ngati inu mwagwera pansi *apa* izo sizikutanthauza kuti inu mwataika. Inu mwangokhala mphungu imene yalowa mu khola, ndizo zonse. Inu mwatsekeredwanso mu khola pansi apo mu tchimo. Inu simukufuna kukhala mmenemo, ndi chifukwa chake inu mukuyang'ana mmwamba. Ndi zimenezotu pamenepo, "Oh, M'bale Branham, ine nthawi ina ndinkakhala kumtunda uko, kodi ilipo njira kuno?" Inde.

120 Zikundikumbutsa ine za tsiku lina, oh, mnyamata wamng'ono, ndinkayenda mozungulira kuseri kwa munda, ndipo apo panali, winawake anali atamangirira khwangwala wakale kuti asamafikire ku chimanga. Ndipo chinthu chosauka chakale chimenecho chinali pafupi kufa ndi njala. Ine sindingakhale wankhanza chomwecho kuchita zimenezo. Iye anamumanga khwangwala wakaleyo pa phazi, ndipo chinthu chakalecho chinadya chirichonse chimene chinali pafupi, iye samatha kupeza china chirichonse, mlimiyo anangomusiya iye. Ndipo iye anali wosauka kwambiri mwakuti iye—iye samatha nkomwe kuti ayimirire. Basi iye. . .Ndipo akhwangwala ankawulukira pamenepo ndikuti, "Kawu, kawu, kawu." Mwakunena kwina, akuti, "Tiye, Johnny Khwangwala! Nthawi yachisanu ikubwera, tiyeni tizipita kummwera!" Koma iye sakanakhoza kuchita zimenezo, iye anali atamangidwa.

121 Kotero tsiku lina munthu wina anabwerapo ndipo anamuwona khwangwala wakale wosauka uja, kotero iye anangopita pamenepo ndi kukamugwira iye ndi kumumasula iye, anati, "Kazipita, mnyamata, ndiwe mfulu." Mukuona? Ndipo kotero ndiye, chinthu choyambirira inu mukudziwa, iye amapitiriza kumayenda mozungulira.

122 Apa akhwangwala anadzabwera, akufuula, "Tiye, Johnny Khwangwala! Kawu, kawu, kawu! Tiye tizipita kummwera, chisanu chikubwera. Iwe uzizidwa mpaka kufa."

123 Ngati iye akanayang'ana mmbuyo, akanati, "Sindingathe kuchita zimenezo." Mwaona, iye anali atazolowera kwambiri kukhala atamangidwa, mwaona, iye ankangoganiza kuti iye anali akadali womangidwa.

124 Inu mukhoza kuganiza kuti ndinu womangidwa, inunso, m'bale, mlongo, amene munalemba funso ili. Inu mukhoza kuganiza kuti mdierekezi wakumangirirani inu pansi apo, koma iye akunama. Inalipo nthawi ina Munthu anabwera pa dziko lapansi, Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, Iye anadzakumasula iwe. Usakhulupirire zimenezo; iwe sukusowa kuti udzikhala pansi pamenepo, ayi, bwana, ndiwe mfulu. Izo nzoona. Iye anafa m'malo mwako kuti adzachotse machimo ako. Iwe ungokhulupirira pa Iye, kazikupiza mapiko akowo ndi kumawulukira kutali ndi ena onsewo. Usakhale mu dzenje limenelo la mdierekezi. Ayi, bwana.

> Tsopano. **Kodi inu mungayike manja pa ine ndi kundimasula ku zimenezo?**

125 Mlongo wokondedwa kapena m'bale wokondedwa, ndithudi, ndingayike manja pa inu, koma izo sizingakumasuleni inu. Chimene chingakumasuleni inu, ndinu. . .ndi kumvetsa kuti ndinu mfulu kale. Munamasulidwa kale. Inu simukusowa kuda nkhawa za kukhala mfulu, ndinu mfulu kale! Yesu anakumasulani inu. Musakodwenso mu goli la ukapolo.

Ndinu mfulu momwe mungakhalire. Inu simukusowa kukhala womangidwa. Kusanjika manja anga pa inu ndi mwambo chabe. Ife tikhoza kuchita zimenezo. Kuti, bwanji, ine ndingakhoze kuchita zimenezo, koma izo sizingakumasuleni inu mpaka inu mutavomereza chimene Iye anakuchitirani inu; zimenezo ndi ineyo kungoti "Ambuye, ine ndikuzikhulupirira Izo."

126 Chabwino, inu mungoyika manja anu mwa chikhulupiriro pa Iye, ndikuti, "Ambuye, ine ndikukhulupirira Izo," apo inu nkubwera. Uko nkulondola, kuwulula machimo anu. Mwaona, "Iye amene abisa machimo ake sadzapindula, kuphimba machimo ake. Koma iye amene adzaulula machimo ake. . . " Apo ndi pamene mumapeza ufulu ndi kulungamitsidwa, pamene ulolera kunena kuti "Ndachimwa, ndalakwitsa." Ndi zomwe inu munanena apa:

> **Ine ndagwa, ine ndachimwa. Ine ndalakwitsa kwathunthu! Kodi pali mwayi woti ndingakhalenso wamphumphu kachiwiri?**

127 Mwamtheradi! Miniti imene inu mwakhumba Izo, izo zikuwonetsera kuti Mulungu anagwetsera Mzerewamoyo pansi kuti adzakunyamuleni inu. Ingodzukani pa Mzerewamoyo Wake wa chikhulupiriro ndi pemphero, sunthirani mmwamba mpaka kwa mphungu zina zonse monga choncho, pitani mukukupizira kutali. Uko nkulondola.

128 Inde, kusanjika kwa manja, ndicho—ndicho chinthu chachikulu, ndimakhulupirira mu zimenezo. Ine ndimakhulupirira mu kusanjika kwa manja, ine ndithudi ndimatero. Koma izo si zomwe zimachita zimenezo. Ine ndikhoza kuyika manja pa anthu, sabata ndi sabata, ndipo komabe izo sizingachite ubwino mpaka inu mutavomereza chimene *Khristu* anakuchitirani inu. Uko ndi kuvomereza kwanga kokha, kusanjika manja. Iwo ankasanjika manja pa maeledara. Iwo ankachita zinthu zimenezo, kunali kuvomereza kwawo pamaso pa Mulungu kuti iwo amapereka chikhulupiriro chawo kwa izo, iwo ankapereka chikhulupiriro chawo kwa zimenezo. Mukuona? Nthawizina, chimodzimodzi monga zinthu. . .

129 Ine sindimamvetsetsedwa nthawi zambiri. Ine—ine ndakhala. . . usiku wathawu. Ndikuyima pakati pa malingaliro, ndipo ine—ine sindikudziwa basi mbali yoti nditembenukireko. Ine—ine ndi, inemwini, ndiri pakati pa malingaliro, ine—ine sindikudziwa choti ndichite. Ine ndikuyembekeza uwu ndi mpingo wachibadwa chabe, kapena mpingo wauzimu umene wakhala pano, kani, ine sindikuganiza kuti iwo akujambula izi kotero ndingonena zomwe ndikufuna kunena. Iwo. . .

130 Ine ndimafuna kuyankhulana kwapang'ono kwa mtima-ndi-mtima ndi inu, ndipo ine ndikukhulupirira ine ndingotenga izo, mulimonse. Ine ndinali ndi cholemba ndalemba apa ndi

Lemba, kaya . . . Ngati ine sindinatero, ine ndimati ndiyankhule pa *Uvangeri Wa Nthawi-Yotsiriza*, chimene uvangeli wa nthawi yotsiriza uli. Mwinamwake ndiwusungira iwo tsiku lina. Ndikufuna ndidzayankhule nanu kuchokera pa mtima wanga, basi kuchokera pansi pa mtima wanga.

131 Ine ndiri pakati pa malingaliro, sindikudziwa mbali yoti nditembenukireko. Ndikufuna pemphero lanu. Kukopana kwapang'ono uku apa, pa izi—pa zinthu izi, kunali kungopeza mwayi woyankhula nanu kwa maminiti pang'ono. Chinachakenso chimene ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu, mwaona. Ine ndikuzindikira kuti ife tiri pafupi kwenikweni ndi chinachake. Tsopano, musandimvetse molakwika ine, musachite zimenezo. Mukuona?

132 Mwamuna anabwera kwa ine tsiku lina ndipo anandipangitsa ine kumverera moyipa kwenikweni. Ine ndinaganiza, "Ndithudi ine sindinakhalepo wolekerera motero mu kuphunzitsa." Mukuona? Iye anati, "M'bale Branham, mu pafupifupi masiku ochuluka chotero ine ndikuyenera kuti ndichitidwe opareshoni, masiku fifitini otsatirawa, twente." Anati, "Kodi inu mukuganiza kuti Yesu adzakhala pano, ine sindidzasowa konse kudzakhala ndi opareshoni imeneyo?" Mukuona? Inu mwaona, inu simunamvetsetse Izo. Musamachite zimenezo! Mwaona, musamachite zimenezo. Yesu akhoza osabwera kwa zaka faivi sauzande zina. Ine sindikudziwa. Iye akhoza kukhala ali pano usikuuno. Iye akhoza kubwera mawa. Ine sindikudziwa ndi liti Iye akubwera, palibe aliyense akudziwa. Kunena moona, ngakhale Iyemwini sakudziwa nkomwe. Icho ndi chimene Iye ananena. Palibe amene akudziwa.

133 Koma kodi mumadziwa kuti Paulo ankayembekezera kuti Iye abwera tsiku lirilonse? Yohane, pa Chisumbu cha Patimo, ankaganiza kuti adzakhala ali moyo kuti adzawone izo. Ireniyasi ankaganiza motsimikiza kuti Iye anali mmasiku ake. Ena onse a iwo, Polekapu, Martin Woyera, onse kudutsa mu m'badwo. Luther ankaganiza, "Ndithudi ndi zimenezo!" Wesley anati, "Iyi ndi nthawiyo." Charles Finney, John Knox, Calvin, Spurgeon, aliyense wa iwo ankati, "Iyi ndiyo nthawiyo!" Billy Sunday, kutsika mmusi mpaka tsiku ili pano, aliyense, "Iyi ndiyo nthawiyo!"

134 Ife tikuyembekezera zimenezo. Ife sitikudziwa kuti nthawiyo ndi liti. Ine ndikukhulupirira kuti ndi nthawi ino, ndipo ndikufuna kugwira nyaliyo. Ndipo mvetserani, ine . . . Gwirani izi molondola! Ndikufuna kumakhala mphindi iliyonse ya moyo wanga kuti ndikumuyembekezera Iye nthawi yotsatirayo, koma ndikufuna kumapitirira ngati kuti zikhala zaka teni sauzande kuchokera pano. Ndikufunabe ndizibzala mbewu, kukolola zokolola. Ine ndikufuna ndizilalikira Uthenga ndi kumapitirira monga ndimachitira nthawizonse. Kumapitirira monga chomwecho, maso anga ali mmwamba, ndikuyang'ana;

kukoka kama wa . . . kutenga mitolo, njere. Ndipo kenako chaka chamawa ine ndidzafetsanso mbewu zanga, "Ambuye, ndimaganiza kuti Inu mukanakhala kuno chaka chatha, koma ngati Inu simutero, Inu mukhoza kubwera chaka chino. Kotero ndibzala mbewu zanga kuti ndizirera nazo ana anga. Ngati Inu muchedwa, iwo adzakhale ndi chinachake choti adzadye; ngati Inu simutero, ndidzakhala ndikukuyembekezerani Inu." Ndi zimenezotu pamenepo, mwaona, muzingopitirira mwachizolowezi.

135 Ngati ine ndikanaganiza kuti Iye abwera mmawawu, usikuuno ine ndikanalalikira uthenga womwewu umene ine ndikulalikira tsopano. Ngati ine ndikanaganiza kuti Iye akubwera mmawawu, ine sindikanapita kunja ndi kukagulitsa galimoto yanga, ine sindikanapita kukachita *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*. Ine ndikanangomapitirira momwe ine ndimayendera nthawizonse, chifukwa mphindi iliyonse ine ndikumuyang'anira kuti Iye abwera. Chifukwa Iye akhoza kubwera chifukwa cha inu basi, zikhoza kukhala kuti ora lanu likhoza kukhala usikuuno. Mwinamwake ndi ora langa usikuuno. Ine sindikudziwa. Koma limodzi mwa iwo lidzakhala ora lathu.

136 Ndipo kodi izo zimapanga kusiyana kotani ngati ine ndikukhala kuno kapena ine ndikaikidwa kunja uko? Pakuti ngati ine ndalipira kale chilango cha imfa, ine ndidzakakhala kumeneko munthu aliyense amene ali moyo asanafike. Uko nkulondola. "Ine ndikunena ichi," Atesalonika Wachiwiri, mutu wa 5, "Ine ndikunena ichi kwa inu mu Malamulo a Ambuye. Ife amene tiri moyo ndipo tidzakhalapo mpaka Kudza kwa Ambuye sitidzawatchinga kapena kuwaletsa iwo amene akugona. Pakuti lipenga la Mulungu lidzalira, ndipo akufa mwa Khristu adzawuka koyamba," mwayi wa iwo amene anafa ndiwoti adzatulukira koyamba. Umo ndi momwe ife timadziwira kuti izo ziri pafupi, mwaona. "Ndiye ife amene tiri moyo ndipo tatsalira tidzasandulika, mu kamphindi, kuphethira kwa diso, ndipo tidzakwatulidwira mmwamba limodzi ndi iwo, kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga."

137 Kotero izo zikupanga kusiyana kotani ngati ine ndikanafa mu nthawi ya Nowa, ngati ndikanafa mu nthawi ya Abrahamu, ngati ine ndikanafa mu nthawi ya atumwi, ngati ndikanafa masabata awiri apitawo, kapena pakali pano? Kodi izo zikanapanga kusiyana kotani? Ine ndidzakhala kumeneko mu kamphindi, mu kuphethira kwa diso, ine ndikungopuma kufikira nthawi imeneyo.

138 Tsopano, kusonkhanako kudzakhala kwa Ambuye. Monga Yakobo, mu mutu wa 49, iye anati, "Pamene Shiloh adzabwera, ndipo kusonkhana kudzakhala kwa Iye. Sipadzakhala wopereka lamulo akupita mpaka . . . kuchokera pakati pa mapazi, kufikira

Shiloh atabwera," akuyankhula za Yuda, "ndipo kwa Iye kudzakhala kusonkhanako."

139 Tsopano, anthu ambiri akufunafuna mpingo, gulu lalikulu la anthu loti adzatengedwere mmwamba pamodzi, mpingo, chipembedzo, kachikhulupiriro kenakake kuti adzatengedwere mmwamba. Izo si zimenezo. Izo si zimenezo nkomwe.

140 Kusonkhanitsidwa kwa anthu, pamene Mulungu adzayitana nkhosa Zake pamodzi, Iye akhoza kudzatenga awiri kuchokera ku Jeffersonville, awiri kuchokera ku Indiana, awiri kuchokera ku Kentucky, awiri kuchokera ku Mississippi. Ndizo ndendende zomwe Iye ananena; osati mawu amenewo, koma Iye anati, "Padzakhala awiri m'munda," ndiko kumene kuli kuwala kwa masana, "Ndidzatenga mmodzi ndikusiya mmodzi. Padzakhala awiri pabedi," mbali ina ya dziko lapansi ndi usiku, "Ndidzatenga mmodzi ndikusiya mmodzi." Mukuona?

141 Kusonkhana kwa anthu sikudzakhala kwa fuko, kwa gulu *pano*. Icho chidzakhala chiwukitsiro cha konsekonse kusonkhana pamodzi, ndipo Mkwatulo udzabwera mwanjira yomweyo. Chifukwa Iye anati, "Pamene wina anagona mu ulonda *uwu*, wina mu ulonda *uwo*, wina mu . . . kupitirira mmusi mpaka ku ulonda wachiseveni. Ndiyeno pamene Mkwati anabwera, onsewo anawuka, aliyense, njira yonse kuyambira nthawi ya Genesis mpaka kumapeto kwa Chivumbulutso. Aliyense wa iwo anadzuka, ndiko kulondola, kukonzekera kuti alowe mkati."

142 Tsopano, inu mwaona, Iye akuwonetsera kuti akufa onse adzawuka kuchokera mmanda, pa kudza Kwake, olungama, Mkwatibwi, iwo ogona amene ali mmanda adzawuka pa chiukitsiro. Kenako Iye akuwonetsera kuti anthu amene akukhala alimoyo padziko lapansi, adzakhala mmodzi *apa* ndi mmodzi *apo*, silidzakhala gulu la anthu osonkhana pamodzi mu gulu laling'ono. "Pakuti padzakhala mmodzi m'munda, kapena awiri m'munda, Ine ndidzatenga mmodzi ndi kusiya mmodzi," apo pakubwera umodzi wa Mpingo kuchokera mu kuwala kwa tsiku. Kumbali ina ya dziko lapansi, "Padzakhala awiri pa bedi, Ine ndidzatenga mmodzi ndipo ndidzasiya mmodzi." Ndi kulondola uko?

143 Kotero kusonkhanako kudzakhala kwa Khristu kaya ine ndiri ku Jeffersonville, kaya ndiri ku Sweden, kaya ine . . . Ndipo kulikonse kumene iko kudzakhale, ndiko kusonkhana komwe kudzakhale kwa M'busa. Mukuona? Ndipo kenako limodzi tidzakwatulidwa ndi chiukitsiro kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga. Anthu adzakhala akubwera kuchokera kumadera onse a dziko lapansi, amene ali a moyo. Anthu amene anafa, ndi zina zotero, adzauka. Ndipo pamodzi Mpingo udzakwatulidwira mmwamba limodzi kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga. Mukuona?

144 Kudza Kwake kudzakhala kwa dziko lonse. Iko sikudzakhala kungobwera ku Louisville. Iko sikudzakhala kungobwera kwa a Baptisti, kwa a Presbateria. Iko kudzakhala "oyera mtima adzamuwona Mulungu," ndipo chiukitsiro ndi kusonkhanako kudzakhala kuchokera konsekonse.

145 Ndipo, tsopano, kodi izo zikubwera liti? Mwinamwake usikuuno, mwinamwake mawa, mwinamwake chaka chino, mwinamwake zaka fifite, mwinamwake zaka handirede, mwinamwake zaka sauzande zina. Ine sindikudziwa. Palibe wina aliyense amene akudziwa. Koma tiyeni—ife, inu ndi ine, tikhale usikuuno ngati izo zichitika usikuuno.

146 Koma, tsopano, pochita monga inu munanenera, "Ine—ine ndiri ndi opareshoni." Chabwino, ngati inu mukuyenera kukhala ndi opareshoni, inu mulibe chikhulupiriro cha kuwomboledwa, pitiririrani kakhaleni ndi opareshoni yanuyo.

147 Ngati ndikanati ndigule a—a. . .Winawake anabwera ndipo anandilembera ine cholemba tsiku lina, ndipo anati, a—kalata yopambana, ndipo anati, "M'bale Branham, ine sindikudziwa choti ndichite." Anati, "Ine ndi mkazi wanga takhala okhulupirika kwa Mulungu momwe ife tikanakhalira. Ife tawalera ana athu." Ndipo anati, "Tsopano, chimene ine ndikudabwa," anati, "ife ta. . .ife tasunga munda, tinagula munda." Ndipo anati, "Momwe ife timawukondera iwo! Kuli kasupe kumeneko; kuli a—khwawa limayenda kudutsa pamalopo." Uko kunali kunja ku Oregon. Ndipo anati, "Ife tamva kuti inu mukubwera ku Oregon. Ine ndikuuzani chimene ife taganiza kuti tichite. Ife tikudziwa kuti. . .Ife tinkaganiza kuti tidzawusungire iwo kwa ana, chifukwa palibe mmodzi wa iwo amene ali Akhristu." Anati, "Ife tinkaganiza kuti tiwusungire iwo kwa iwo chifukwa iwo akuyenera adzatsala kuno kuti adzadutse mu chisautso, ndi kusunga iwo chifukwa cha iwo ndi kuwalola iwo adzatsale ndi chinachake, pakuti ife tikukhulupirira kuti ife tidzakhala mu Mkwatulo. Chotero ife sitikudziwa choti tichite pa zimenezo, kotero mwinamwake mukabwera tidzangopereka mundawo kwa inu, mwaona, ndipo kenako inu mukhoza kudzachita nawo chirichonse chimene inu mukufuna kuchita."

148 Ine ndinalemba powayankha, ine ndinati, "Ndi zabwino bwanji kuti munawaganizira ana anu."

149 Anati, "Ine ndi amayi timapita kumeneko, ndipo madzulo." Anati, "Ine ndakonzeka kuti ndipume ntchito, ndipo," anati, "maola osangalala amene ife tiri nawo, timakayendayenda mmundamo, kukayang'ana pa kasupeyo, ndi kukayima kunja uko tikumuyamikira Mulungu."

150 Ine ndinati, "Kazipitirizani kumachita zimenezo, muzingokhala mwanjira imeneyo basi, mwathupi, mwazinthu. Kazingopitiriranibe kumangopitirirabe mpaka Iye adzafike.

Mwaona, muzingopitirirabe kumakhala kuno, kumapitirirabe mpaka Iye adzafike."

151 Konzekerani, kazipitirirani, kumapanga zimenezo, "Ngati Ambuye alola! Ngati Ambuye alola! Ine ndichita *ichi*, ngati Ambuye alola." Iye akhoza kubwera nthawi imeneyo isanafike. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Koma kazingopitirirani kumangopitirira monga momwe inu mukuchitiramo mpaka . . . Koma muzikonza moyo wanu, kuti, Iye akhoza kubwera pa miniti iliyonse. Mwaona, zikhalani okonzeka. Pakuti, inu mwaona, Iye akhoza kubwerera *inu* miniti iliyonse, sekondi iliyonse, kugunda kwa mtima kotsatira, kupuma kotsatira, Iye akhoza kubwerera inu. Koma kazipitirirani kuchita chirichonse chimene inu mukufuna, bola ngati icho chiri choona ndi choyenera ndi chowongoka, pitirirani ndi kuchita icho.

152 Tsopano, ife tikudziwa kuti ife tikuyang'anizana ndi chinachake. Ine ndikudziwa zimenezo; inu mukudziwa zimenezo. Ine—ine—ine sindikudziwa njira yoti nditembenukireko. Inu mukukumbukira pafupifupi zaka foro zapitazo, mu Chicago tsiku lina, Mzimu wa Ambuye unabwera pa ine ndipo ine ndinati, "Ichi ndi chimenecho! Ndipo chitsitsimutso chatha, ndipo Amerika wakana mwayi wake." Izo ziri pa tepi. "Ndipo sipadzakhalanso. Mwayi wake womaliza iye anawukana."

153 Ndikufuna kuti inu muwone. Kodi aliyense akudziwa tsiku limene ilo linali pa tepi? Ife tiri nayo iyo. Leo ndi Gene ali nayo. Ine ndinazimva izo kuno osati kale. Boze analemba izo mu pepala lake. Ndipo kotero tangowonani zimene zinachitika kuyambira pamenepo, mwaona, chitsitsimutso chayima.

154 Ine ndinanena zimenezo ku—ku Blue Lake usiku wina, ndipo mnyamata wamng'ono anadzabwera mmawa wotsatira, anati, "M'bale Branham akhoza kunena kuti Achipentekoste anakhalapo nazo izo, koma osati ine! Ulemelero kwa Mulungu! Aleluya," ndi kumapitirira. Mwaona, koma mnyamata wamng'onoyo sankadziwa basi mapeto a lipenga limene iye ankawombako. Mwaona, iye samamvetsetsa. Mwaona, iye sakudziwa. Izo ziri bwino, anatengeka, izo ziri bwino mwangwiro.

155 Koma yang'anani pozungulira! Iwo akuchita chiyani? Vuto ndi chiyani ndi anthu? Kodi chachitika ndi chiyani kwa chitsitsimutso? Chachitika ndi chiyani kwa Billy Graham, Oral Roberts, ena onse a iwo? Kodi chitsitsimutso chikuchitikira kuti? Icho chatha! Utsi wakhazikika. Mbewu zafesedwa. Msonkhano watha. Moto wazima. (Mu kachisi wakale wa Roma, mu vesta, pamene moto unazima amalonda anapita kwawo, pa maguwa.) Tsopano, ife tikuwona kuti chitsitsimutso chatha. Si kutengekako.

156 Ndiye ine ndikuganiza za mtsinje mu 1936, ndikuganiza chimene Iye ananena. Kodi chinachitika ndi chiyani kumeneko? Ambiri a inu mukudziwa. Ine ndinali mnyamata chabe, ndipo ndikubatiza ubatizo wanga woyamba pamene Mngelo wa Ambuye uja anabwera kumeneko ndipo anadzayima pamene ine ndinali. Anthu ena anati, "Inu simunaziwone izo." Kenako sayansi inadzatsimikizira kuti izo zinali chomwecho. Mukuona? Mukuona?

157 Tsopano, kodi Iye ananena chiyani pamenepo? "Monga izo zinali, monga Yohane M'batizi anatumizidwa kuti adzatsogolere kudza koyamba kwa Khristu, Uthenga wako udzatsogolera Kudza kwachiwiri."

158 Ine ndachiwona icho kudutsa padziko lapansi, kuzungulira dziko icho chinapita. Basi pafupifupi usiku wokha, zitsitsimutso zinayambika konsekonse. Moto wa chitsitsimutso unkayaka kulikonseko, pakhala pali chitsitsimutso chachikulu kwambiri chimene ife tinayamba tachidziwapo. Koma kodi panali kalikonse izo zisanachitike? Panalibe kanthu! Pamene masabata awiri izi zisanachitike, ndinamumva munthu akuyankhula ku New Albany, anati, "Anthu ankakhulupirira kuti phokoso la—la chitsitsimutso, monga Billy Sunday ndi iwo." Anati, "Ife tikudziwa kuti sipangakhalenso ena a iwo. Anthu akufuna umboni wogwirika; palibe chinthu choterocho!" Pamene iwo ankapanga phokoso lalikulu limenelo, pa nthawi yomweyo Mulungu anaphulitsa chitsitsimutso chachikulu kwambiri chimene ife tinali nacho kuyambira zaka zawo zoyambirira, anthu ochuluka apulumutsidwa: mamillioni.

159 Ziwerengero zimawonetsa kuti uthenga wa munthu umatenga zaka zitatu, aliyense wa iwo, kenako iye amakhala moyo pa mbiri yake nthawi yonse yotsala mpaka Mulungu atamuyitana iye. Tsopano, zimenezo zakhalapo kuyambira pa Khristu, Wake unali zitatu ndi theka, mwaona. Ndi kuziwonetsa izo zonse kutsika pansi, Spurgeon, Knox, Calvin, njira yonse kumatsika mmusi, izo zimasonyeza zaka zitatu mpaka zitatu ndi theka ndiwo malire a utumiki wa munthu. Zina zonsezo. . .Kandulo yake yayaka, iye akukhala pa mbiri yake yakale. Ngati iye wakhala ali woyipa, zake—ntchito zake zimamutsatira iye; ngati iye wakhala ali wabwinobwino, ntchito zake zimamutsatira iye. Ndizo zonse.

160 Tsopano, kodi zimenezo zimatanthauza chiyani? Ine ndakhala ndikulalikira ku mpingo uwu kuno ndi kumakuuzani inu kuti "Ndimakhulupirira kuti panali wina wamkulu akubwera." Ine ndikukhulupirira ndipo ndakuuzani inu kuti "Ndimakhulupirira kuti Malemba amathandizira kuti padzakhala mtumiki wa m'badwo wa mpingo wotsiriza." Ine ndikukhulupirira zimenezo. Ine ndakhala ndikuyang'anira kuti munthu ameneyo awonekere, ndayang'anira mosalekeza.

161 Ndipo ine ndikawona munthu akudzuka, ndimamva za iye, munthu wamkulu akayamba kusesa, ine ndimazindikira kuti uthenga wake ukutalikirana ndi Baibulo. Ine ndimamuwona iye akuwulukira mmbuyo mu ngodya. Mukuona? Ine ndimamuwona wina akudzuka, akuwulukira kutsidyako, koma iye samafika pakati pa mphungu, iye amakakhala pakati pa akhwangwala achipembedzo. Amakakhala pansi *apa*, bungwe lake, ndipo wina amabweretsa mamembala ochuluka ndi zina zotero. Ine ndimayang'ana izo, ndimaziwona izo zikufa.

162 Ine ndimaganiza, "Mulungu, ali kuti mmodzi ameneyo amene ati adzabwezeretse Chikhulupiriro cha atate kwa ana? Mbewu zimenezo zidzabzalidwa kuti? Izo ziri kuti? Ndi chiti chidzachitike?"

163 Tsopano izo zimafika kwa ichi. Ngati—ngati Uthenga umenewo pa mtsinje tsiku limenelo, ngati unali umenewo, Kudza kwa Ambuye kwayandikira, kuli pafupi ndi pano. Ngati iko sikuli, pamakhala bata kusanakhale mkuntho. Ine sindikudziwa. Iye sanaulule izo kwa ine. Ndikuyesetsa kudabwa, "Kodi umenewo unali Uthenga Wake wovomerezeka? Kodi izo ndi zonse zomwe Iye amafuna kuti ine ndinene? Kodi apo panali pamene Iye anatuma? Kodi izo zinali zonse za izo? Ngati izo ziri, ife tiri kwenikweni, pafupi kwenikweni. Ndi mochedwa kuposa momwe mukuganizira. Ngati izo sizinali, pamakhala bata mkuntho usanachitike.

164 Tsopano, winawake anandilembera ine kuno osati kale, ndipo anandifunsa ine, anati, "Ngati inu simumakhulupirira kuti mpingo udzadutsa mu nthawi ya Chisautso, nanga bwanji Chivumbulutso 13, momwe iwo anagonjetsera ndi Magazi a Mwanawankhosa ndi umboni wawo?" Munthuyo anafunsa funso limenelo. Ine ndikudabwa. Kodi inu mukuzindikira kuti mitu itatu yoyamba ya Chivumbulutso imachita ndi Mpingo mu m'badwo wa Mpingo? Imeneyo ndi nthawi ya Chisautso, osati m'badwo wa Mpingo; Mpingo Ukukwatulidwa ndi kupita mmwamba pa mutu wa 4 wa Chivumbulutso, sukubwereranso mpaka mutu wa 19 pamene Iwo ukubwera ndi Yesu. Uko nkulondola. Umo ndi mu nthawi ya Chisautso, osati kanthu kochita ndi Mpingo nkomwe.

165 Malonjezo onse aakulu awa a zinthu zazikulu zimene inu mwaziwona mu Baibulo, monga chimene chiti chidzachitike, zimenezo ndi uko mu ufumu wa Chiyuda, osati kuno pakati pa Amitundu. Ine ndikukhulupirira kuti iwo adzakhala ndi kusonkhana ndi uyu amene akuyenera kubwera kuti adzabwezeretse Chikhulupiriro cha anthu, chimene chinalonjezedwa. Ndipo njira yokhayo imene ine ndingathe kuzipezera zimenezo, chifukwa Iye anati, "Mwamsanga ukadzatha Uthenga uwu, kuti, dziko lapansi lidzawotchedwa ndi kutentha, moto." Ndiroleni ine ndingowerenga izo kwa

inu pamene ife tiri pomwe pano, ndipo muwone chimene Iwo ukunena.

166 Ndipo tsopano Uthenga wawung'ono uwu wa Ufumu, mwinamwake ine ndikhoza kudzaulalikira iwo Lamlungu likudzali mmawa, ngati Ambuye alola, mwaona, ndipo ngati Ambuye alola.

167 Tsopano penyani apa, uku ndiko kudza kwa Yohane, Malaki 3:

> *Taonani, ine . . . nditumiza wamthenga wanga* pamaso pa Wanga . . . *nditumiza wamthenga wanga, ndipo iye adzakonza njira pamaso panga: ndipo Ambuye, amene inu mukumufuna, adzafika modzidzimutsa ku kachisi wake, ngakhale wamthenga wa chipangano, amene inu mukondwera naye: taonani, iye adzabwera, atero* AMBUYE *wamakamu.*

168 Inu mukuona zimenezo? Malaki 3. Mateyu tsopano, penyani Mateyu mutu wa 11, ndipo mvetserani kwa izi, ndi ndime ya 6. Tiyeni tiwerenge tsopano Mala- . . . Mateyu 11, Yesu akuyankhula. Ndipo tsopano tiyeni tiyambire pa mutu wa 11:

> *Ndipo zinafika pochitika, pamene Yesu anamaliza kuwalamulira ophunzira* Ake *khumi ndi awiri, iye anachoka kumeneko kupita kukaphunzitsa ndi kukalalikira m'mizinda yawo.*
>
> Ndipo *tsopano pamene Yohane anamva mu . . . m'ndende ntchito za Khristu, iye anatumiza awiri a ophunzira ake,*
>
> *Ndipo anati kwa iye, Kodi inu ndi iye amene amayenera kudza, kapena tiyembekezere wina?*

169 Mukuona kulunda kumeneko kwa mneneri ameneyo? Iye ankadziwa kuti chinachake chikanati chichitike, koma iye sanali wotsimikiza pamene izo zinali, mwaona, mwaona, basi chimene chinkachitika. "Kodi Inu ndi Iyeyo?" atatha kumulengeza Iye.

> Ndipo *Yesu . . . ananena kwa iwo, Pitani ndipo* mukamuwonetse *Yohane kenanso zinthu zimenezo zimene* inu *mukuzimva ndi kuziwona:*
>
> *Akhungu akulandira kupenya kwawo, . . . olumala akuyenda, akhate akuyeretsedwa, . . . ogontha akumva, akufa akuwukitsidwa, ndipo osauka ali ndi uthenga ukulalikidwa* kwa *iwo.*
>
> *Ndipo wodala ndi iye,* amene *sakhumudwa mwa ine.*
>
> *Ndipo pamene iwo anapita, Yesu anayamba kunena kwa* khamu *za Yohane, . . .* (Tsopano mvetserani!) . . . *Inu munapita kunja mchipululu kukawona chiyani? Bango logwedezeka ndi mphepo?* (Ayi, ameneyo sanali Yohane, panalibe kunyengerera ndi Yohane.)

> . . .*inu munapita kunja kukawona chiyani? Munthu wovala zovala zofewa?* (Mwa kuyankhula kwina, kolala yotembenuzidwa, inu mukudziwa, ndi wophunzira ndi munthu wamkulu) *taonani, iwo ovala* zovala *zofewa ali m'nyumba za mafumu.* (Iye amene amapsyopsyona khanda, ndi kukwatitsa ana, ndi kuyika akufa, ndipo, inu mukudziwa, kapena kukhala pafupi ndi mafumu. Umenewo ndiwo mtundu umenewo, iye sagwira Lupanga la manja awiri. Mukuona?)

> . . .Tsopano, *kodi munapita kunja mchipululu kukawona chiyani?* Munthu ndi zovala zake, ndipo *wogwedezeka ndi mphepo?*

> . . .*Munthu wovala zovala zofewa? taonani, iwo amene amavala zovala zofewa ali* m'nyumba *za mafumu.*

> *Koma inu munapita kunja kukawona chiyani? mneneri? eya, Ndinena kwa inu, ndipo woposa mneneri.*

170 Penyani! "Pakuti uyu. . ." Mvetserani tsopano, awa ndi Mawu Omwe a Yesu:

> *Pakuti uyu ndi iye, kwa amene kunalembedwa, Taonani, ine nditumiza wamthenga wanga patsogolo pa* Chikhulupiriro Changa, ndipo iye. . .nkhope, ndipo iye *adzakonza njira pamaso panu.*

171 Tsopano penyani Malaki 3:

> *Taonani, Ine. . .nditumiza wamthenga wanga, ndipo iye adzakonza njira pamaso Panga:*. . .(Malaki 3, osati Malaki 4.)

172 Tsopano penyani Malaki 4:

> *Pakuti, taonani, tsiku likudza, limene lidzayake ngati ng'anjo; ndipo onse odzikuza, eya, ndi onse akuchita zoipa, adzakhala* ziputu:. . .*tsiku* likudza limene *lidzawawotcha iwo, atero* A*MBUYE* *wa makamu,*. . .*ilo* sili*dzawasiyira iwo muzu kapena nthambi* (zimenezo ndi za Chisautso ndi chiwonongeko, mwaona, zimene ziri nkudza).

> *Koma kwa inu akuwopa dzina langa Dzuwa la chirungamo* lidzatulukira *ndi machiritso m'mapiko ake* (kudza kwa Ambuye); *ndipo inu mudzapita* ngati. . . inu *mudzapita, ndipo mudzakula ngati ana a ng'ombe a m'khola.* (Izo ziri ngati kupita ku msipu, nkutulukako.)

> . . .*inu mudzawapondereza oyipa; pakuti iwo adzakhala maphulusa pansi pa zidendene za mapazi anu mu tsiku* limenelo *limene Ine ndidzachita ichi, atero* A*MBUYE* *wa makamu.*

173 Mwa kuyankhula kwina, olungama, pobwerera ndi Khristu padziko lapansi, azidzaponda phulusa. Pamene inu muwawona

anthu amenewa, odzikuza, amwano, onyoza, achipongwe, ndipo komabe kumadzinenera kuti ndi Akhristu, iwo si kanthu koma phulusa. Ndizo zonse. Icho ndi chimene Lemba limanena. Mukuona? Tsopano penyani.

> *Kumbukirani*. . .*lamulo la Mose wantchito wanga, limene ndinalamulira*. . .*iye ku Horebu kwa Israeli yense, ndi malangizo ndi ziweruzo.*
>
> *Taonani, Ine ndidzatumiza* kwa *inu Eliya mneneri lisanadze tsiku lalikulu* limenelo *ndi lowopsya la Ambuye:*

Lisanafike Tsiku limenelo, kubwerera kwa Ambuye, Eliya adzabwera poyamba.

174 Chabwino, kumbukirani, komabe mtsogolo. Tsopano, uko sikukanakhala kubwera kwa Yohane. Iye anali Eliya, koma iye akubwera ka faivi, tsopano. J-e-s-u-s, f-a-i-t-h, g-r-a-c-e. Mwaona, *faivi* ndi nambala ya "chisomo." Eliya akupanga kuwonekera kusanu: nthawi imodzi ndi Eliya; monga Elisha; monga Yohane; kumapeto kwa Amitundu; ndipo uko ndi Mose kwa Ayuda. Nambala yangwiro, mneneri wangwiro, mtumiki wangwiro, wolimba mtima, wosaopa. Mukuona? Zindikirani:

> . . .*Ine ndidzatumiza* kwa *inu Eliya*. . .*lisanadze* Tsiku, *tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye*:
>
> *Ndipo iye adzatembenuza* mitima *ya atate kwa ana, ndi* mitima *ya ana kwa atate, kuti ndingadze ndi kukantha dziko lapansi ndi themberero.*

175 Mwaona, osati kudza koyamba kwa mawu oyamba; ameneyo anali Yohane, chifukwa dziko silinatenthe ngati chiputu, wolungama sanayende pa phulusa la oyipa. Koma izi zisanachitike, Elisha adzabwera. Ndipo kodi iye adzachita chiyani? Kubwezeretsa Chikhulupiriro cha ana kubwerera kwa atate, Chikhulupiriro chapachiyambi cha Baibulo.

176 Ndikawona munthu akubwera, ine ndimaganiza, "Ameneyo akuyenera kukhala iye. Apo pali mwamuna akuwuka mu kutchuka, tayang'anani pa iye, mipingo ikupita." Kodi iye akuchita chiyani? Mailosi sauzande kuchoka pa Baibulo. Iye akuchita chiyani? Akuyendayenda mozungulira, mpweya umatuluka ndipo amapita kumeneko. Mwaona, "Kukhala ndi mawonekedwe aumulungu ndi kumakana Mphamvu yakeyo." Kukana Chikhulupiriro, osakhulupirira mu Baibulo, kumanena, kumagwiritsitsa ku tizikhulupiriro, zipembedzo, kupeza ana achipembedzo. Izo zikuyenera kugwa. Apo iye akubwerera mmbuyo momwe.

177 Ali kuti uyo amene ati adzafese Mbewu imeneyo kwa Mpingo wa nthawi-yotsiriza uwo? Kodi Mbewu yakucha ija ili kuti, Eliya wolonjezedwa uja? Ndipo mwamsanga akadzatha masiku

ake Chisautso chachikulu chidzabwera ndi kudzawotcha dziko lapansi.

178 Ndipo kenako pa kubwerera kwa Mpingo ndi Mkwatibwi, Mkwatibwi ndi Khristu adzayenda pa maphulusa awo, mu Zakachikwi, pamene dziko lapansi lidzayeretsedwe ndi moto. Ndipo kumeneko iwo adzalamulira. Ndipo achikunja amene sanayambe amvapo Uthenga adzaukitsidwa mu nthawi imeneyo, ndipo ana aamuna a Mulungu adzawonetseredwa. Ngati iye ati adzalamulire, iye akuyenera kudzakhala ndi chinachake choti adzalamulirepo, iye ali ndi dera lolamulirapo. "Ndipo iwo analamulira ndi kuchita ufumu limodzi ndi Khristu," ndipo Khristu analamulira ndi ndodo yachitsulo, mafuko. Ndiye Uthenga . . . Ndiye ana owonetseredwa a Mulungu, ndi ulamuliro monga Iye anali nawo pamene Iye anali kuno, mwaona, padzabwera Zakachikwi mu Ulamuliro umenewo, mwaona, pa maphulusa.

179 Kotero ine ndakhala ndikuyang'ana chinachake. Kodi icho chinatizembera ife mu kudzichepetsa ndipo tachiphonya icho? Kodi icho chapita ndipo mpingo wasiyidwa mu machimo ake? Ngati izo ziri chomwecho, ndiye kuti ndi mochedwa kuposa momwe mukuganizira. Ngati sichoncho, ndiye pakubwera wina ndi Uthenga umene uli molunjika pa Baibulo, ndipo ntchito yofulumira idzazungulira dziko lapansi. Mbewu zidzapita mu nyuzipepala, zinthu zowerengera, mpaka Mbewu yokonzedweratu iliyonse ya Mulungu itawumva Iwo. Palibe aliyense wa iwo ati adzabwere kupatula Atate atawakoka iwo, ndipo aliyense amene Atate amukoka adzamva Iwo ndipo adzabwera. Izo zidzakhala, Mbewu yokonzedweratu idzamva Mawu.

180 Kenako pamene izo zichitika, kudzakhala kusonkhana limodzi. Ndipo Yesu adzawonekera, ndipo kumeneko kudzapita Mpingo kuchokera ku dziko lonse lapansi monga chomwecho, ndi chiukitsiro, kupita mmwamba.

181 Kodi izo zidzakhala monga Yohane anabwerera, ndipo ngakhale ophunzira osankhidwa sanadziwe nkomwe izo? Iwo anati, "Ndi chifukwa chiyani alembi amanena kuti Eliya akuyenera kubwera poyamba?"

182 Iye anati, "Iye anabwera kale ndipo inu simunadziwe izo." Koma anati, "Iwo anachita zimene iwo ananena kuti akanadzachita kwa iye." Uthenga wake unali wachangu kwambiri, penyani, kwa Israeli yense, ndipo izo zinachitika mu amodzi aang'ono ma- . . . awiri—magawo awiri aang'ono: basi mmusi mwa Yerusalemu ndi uko, kapena kumusi ku Ainoni kumene Yohane anapita kukabatiza, ndi kumusi komwe pa mtsinje kumene iye ankabatiza, mtsinjewo unawuma. Miyezi sikisi yokha, ndipo kufotokozera konse kwa Mesiya kunabwera mkati momwe. Mukuona?

183 Kodi ife taphonya chinachake? Kodi ndi mochedwa kuposa momwe tikuganizizira? Uku ndikukambirana kwa mtima ndi mtima tsopano. Izi ziri, usikuuno basi, basi ku . . . Eya, ndi basi—ife tikungoyankhula pano. Kodi ndi mochedwa kuposa momwe mukuganizizira? Kodi umenewo unali kwenikweni Uthenga uja pa mtsinje tsiku lija? Kodi iwo wazembera, ndipo anthu awuphonya Iwo? Kodi izo ndi Umenewo? Ndiye ndi mochedwa kwenikweni kuposa momwe tikuganizizira. Izo zidzakhala liti? Ine sindikudziwa. Zikhoza kuchitika usikuuno. Zikhoza kukhala zaka zina fifite. Ine sindikudziwa kuti izo zidzachitika liti, ndingopitirira kupita momwe ndiriri tsopano. Chabwino, icho ndi chiyani? Kodi ine ndikuyembekezera chinachake?

184 Ndinali ndi loto lachilendo usiku watha, ilo landivutitsa tsiku lonse. Kawirikawiri sindimalota kwambiri. Koma ndinali ndi loto . . .

185 Ine ndinkapita kulikonse, ndipo zinkakhala kuti ine ndinkaphulitsa Uthenga umenewo ndipo ine ndinkakhoza kuwona mmodzi apa ndi mmodzi apo akuwugwira Iwo. Ine ndimabwerera mmbuyo kachiwiri ndi kudzaphulitsa Uthengawo ndipo iwo amakweza mphuno zawo ndi kuchokapo. Vuto ndi chiyani? Kodi iwo achimwira tsiku lawo la chisomo? Kodi wotsiriza walowa? Kodi izo zatha? Kodi ife tikungoyembekezera chiwonongeko? Kodi nkhondo zazing'ono zonsezi zikuwuka monga choncho zikungokonzekera?

186 Chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Icho chisanachitike, Mpingo udzapita. Momwe ine ndimatsutsira zoti Mpingo udzakhala mu Chisautso! Inu mungakhoze bwanji kupanga choyimira kuchokera ku chenicheni? Mukuona? Nowa anali mu chombo dontho limodzi la madzi lisanagwe nkomwe. Loti anali kunja kwa Sodomu moto usanagwe konse. Mukuona? Yesu anati, "Monga izo zinali mmasiku amenewo chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu." Mpingo sukusowa kuti udzayime pa chiweruzo, iwo uli kale mwa Khristu.

187 Chimene ife tikusowa ndi ungwiro wa oyera. Oyera sakumvetsa, mwaona, iwo akupeza . . . Iwo sakudziwa basi choti aganize, mwaona. Tsopano ife tiri . . .

188 Ngati izo ziri zolondola . . . Ngati izo siziri, pakubwera chinachake mwamsanga ndithu, padzakhala kuphulika. Ine ndikuyang'ana, sindikudziwa njira yoti nditembenukireko.

189 Usiku wathawu ndinalota loto. (Ndiye ndikutseka.) Ine ndinalota loto, chinthu chodabwitsa kwambiri . . .

190 Ndinali nditagona pamenepo ndikuyankhula ndi mkazi wanga, za kudza- . . . Ife tinali titangopemphera, ndipo ine . . . Winawake, Dallas wamng'ono, anayimba kuti anayika chinachake m'khutu mwake, ndipo ndinakalowa . . . Akutuluka magazi, ndipo amayenera kuthamangira kwa adokotala. Ndipo

ine ndinapita kukapemphera, ndipo Mzimu Woyera unati, “Izo zonse ziribwino.” Mukuona?

191 Apa iye akubwera, izo zonse ziri bwino. Dokotala anati, “Bwanji, ine ndimaganiza kuti iwe ukhala ndi. . . ” Anati, “Iwe wavulaza ng’oma ya m’khutu, yaphulika, ndipo magazi akutuluka kuchokera mmenemo, ndipo zina zonse.” Basi zonsezo. . . Nthawi yotsatira imene tinapita—tinabwerera, iye sananene kanthu za zimenezo. Sankadziwa chiyani, mwaona, panalibe matenda, panalibe kanthu. Mukuona?

192 Kotero ndiye winawake anayimba, ndipo ine ndimatha kupita mchipindamo ndi kukapemphera. Pafupifupi tsiku lina iwo amatha kuyimba, nkuti, “Izo zonse zatha. Wachira ndipo alibwino! Kumapitirira!”

193 Ndipo ndinali kuyankhula ndi mkazi wanga, ine ndinati, “Wokondedwa, kwa pafupifupi chaka ndi miyezi foro ine ndakhala ndisakudziwa kuti ndilowere kuti.” Ine ndinati, “Ine sindikudziwa chiyani.” Iye anati. . . Ife timakambirana za kusuntha, ine ndinati, “Ine sindikudziwa choti ndichite, ndaimirira ndipo ndikudabwa, ‘Kodi ife tikuyembekezera. . . ? Kodi ameneyo ndi mneneri m’modzi wamkulu wa Mulungu amene akubwera powonekera kuti adzachiphulitse chinthucho, kodi icho chidzadziwika kwa gulu?’”

194 Ine ndinaganiza, “Izo ndi zotsutsana ndi Lemba. Ayi, izo ndi: ‘Iye amabwera mu ora limene simukuliganizira.’” Mukuona? Ndipo ndinaganiza, “Ine sindikudziwa choti ndichite. Kodi ife tachiphonya icho?” Ine ndinaganiza, “Ine sindikufuna kukhala pakhomo pano.” Ine ndinaganiza. . . Ndipo ine ndikuyembekeza kuti izi sizikujambulidwa; ngati zikutero, mudzang’ambe tepiyo kapena muyisiye iyo pambali. Mukuona? Tsopano iye anati, ngati. . . Ine ndinati, “Ngati izi ziri zimenezo, ife tiri pafupi kuposa momwe tikuganizira.”

195 Pali chinthu chimodzi chimene chi. . . chimene chiti chidzachitike. Mwina chinachake chikuyenera kuchitika kwa ine tsopano. Ndipo sindikuwona chifukwa chimene Iye basi sanandilole ine kuti ndipite pamene ine ndinali pansi pa benchi imeneyo tsiku lina, ndiye, onani, ngati palibe chinachake choti ndichite. Bwanji? Chifukwa chiyani ine sindinapite? Chinachitika ndi chiyani? Kodi pali china choti ndichite? Ine ndinaganiza, “Chabwino, ngati uli Uthenga wanga, anthu adzatembenuzira mphuno zawo kwa Iwo.”

196 Ndiyeno, Chinachake chikundiyitanira ine ku ntchito ya kunja. Ndikumva kuyitana kutsidya la nyanja, kukubwera kuchokera konsekonse.

197 Kalata inangobwera kumene tsiku lina, M’bale Ligger analemba a—bukhu la msonkhano waku Durban. Iye anati, “Izo sizinafaniziridwepo. Afrika sanayambepo wakhala ndi kugwedeza monga chomwecho. Mu nthawi yausiku umodzi

dziko lamdima ili la Afrika linali ndi kugwedeza kumene sanakhalepo nako m'moyo wawo." Uko nkulondola, uko pakati pa achikunja.

198 Ine ndinayang'ana pansi apo, ine ndinawawona akuda osauka amenewo, anthu ofunika, ndinawona momwe anthu amenewo ankawachitira iwo monga . . . moyipa kuposa akapolo. Ndinawona mnyamata wamng'ono pamenepo amene . . . ndipo ine . . . ankagwira ntchito kumeneko, ndipo ine ndinati . . . Mnyamata ameneyo, iwe basi . . . Akazi inu simukanatha kuchita zambiri m'masiku awiri [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. kapena masiku atatu, molimbika momwe inu mukanakhoza kugwirira ntchito, monga mnyamata ameneyo ankayenera kuchitira mu tsiku limodzi. Iye ankagona pa mphasa kunja mu chimbudzi chaching'ono chakale, pafupifupi kutalika mapazi foro ndi mapazi anayi mu lifupi, atapiringizika pamenepo. Ndipo ankapeza paundi pa mwezi, amenewo ndi madola awiri ndi masenti eyite. Ndipo iye sankadya zinyenyetswa za pa gome, ndowa ya ufa; magawo atatu a iwo, kadzutsa; magawo atatu a izo pa chakudya chamadzulo; ndi magawo atatu ena usiku umenewo pa mgonero. Ankagwira ntchito mpaka teni, kapena leveni, thwelofu koloko; kudzuka m'mawa wotsatira kumusamalira mwana ndi china chirichonse, ndi kupukuta masitepe ndi kupukuta galimoto ya abwana. Ndipo mayi wamkulu, wokalamba, wonenepa samachita kalikonse koma kukhala pamenepo ndi kumadula zikhadabo zake ndi kumwa tiyi, waulesi, wopanda ubwino.

199 Mnyamata wosaukayo ankayenera kugwira ntchito monga chirichonse. Iye anali ndi chifuwa, ndipo iye ankawoneka ngati anali pafupi kuzizidwa, ngati "*Humph*, *Humph*, *Humph!*" Tsiku lina ndinayang'ana kudutsa kumeneko, ine ndinati, "Usadzakhalenso ndi mnyamata ameneyo . . . ? Bwanji osabwera naye ku msonkhano?"

200 "Iye ndi mkafiri." [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Izo zimatanthauza "wopanda khalidwe." Nzosadabwitsa iwo amakhumudwa nalo dzina limenelo. Ine ndingatero, nanenso. Munthu ameneyo ndi m'bale wanga. Ndipo apo iye ali. Iye si kapolo. Mtundu wake ulibe kanthu kochita ndi izo. Iye ndi mchimwene wanga. Ndipo apo iye anali monga chomwecho.

201 Ine ndinatuluka, ndinamutcha iye "Thomas." Mnyamatayo amakhoza kuyankhula zinenero zitatu. Ndipo ine ndinati, "Thomas?"

202 Iye anatembenuka pamenepo, anagwada pa mawondo ake ndipo anakweza manja ake mmwamba, anati: "Inde, mbuye."

203 Ine ndinati, "Imilira. Ine sindine mbuye wako, ndine m'bale wako." Ndinayika nkono wanga momuzungulira iye. Iye anayang'ana pa ine monga chomwecho, ndipo misonzi yayikulu kwambiri ikutsika pa masaya ake. Ine ndinati, "Thomas."

204 Ndipo Mzimu Woyera unadza ndipo apo panali masomphenya. Ine ndinamuuza iye chinachake. Ndipo iye anati, "Inde, mbuye. Izo ndi zoona. Ndizo basi zomwe zinali."

205 Ine ndinati, "Tomasi, chifuwa chakusiya iwe, sudzakhala nachonso." Ndipo iye sanatero.

206 Anthu akulowetsa ndalama mthumba mwanga, ndinali ndi pafupifupi handirede ndi eyite ya ndalama za *paundi* zimenezo (zikutanthauza madola awiri ndi masenti eyite). Ndipo ndimawopa kuti ndipereke izo kwa iye; kuwopa kuti abwana akanamupeza iye ndi zimenezo, iwo akanaganiza kuti iye waba izo ndipo kenako akanamumenya mpaka kufa. Ndiye ine—ine ndinati kwa abwana, ine ndinati, "Ine—ine ndikumukonda mnyamata ameneyo. Ndiloleni ndimupatse iye ndalama."

"Oh, ayi! Ayi! Inu mumuwononga iye."

207 Ine ndinati, "Inu ndi owonongedwa bwino ndithu." Mukuona? "Kodi mukukhalira chiyani kuno? Ndipo simukuchita kalikonse. Mnyamata ameneyo amagwira ntchito zonse ndipo inu mumamusiya pafupi kufa ndi njala. Iye ali ndi—mayi wamasiye ndi mlongo wodwala, ndiyeno inu mumamulola iye azilandira dola . . . madola awiri ndi masenti eyite pa mwezi." Ine ndinati, "Inu mudzakolola tsiku lina chifukwa cha zimenezo! Pali azungu thuu millioni ndi achikuda pafupifupi handirede millioni. Inu mudzakhala ndi kuwukiridwa."

Anati, "Musati mukanene izo ku America, zomwe zikuchitika kuno."

208 Ine ndinati, "Ndani adzandiuze ine kuti ndisunge bata langa? Mulungu yekha." Ndinati, "Nzosadabwitsa kuti anthuwo ali ndi kuyipidwa, pochitiridwa monga choncho." [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Ndi zimenezotu pamenepo. Ndipo ndinawaimira iwo kumbuyo.

209 Tsiku lina atumiki angapo, makolala otembenuzidwa, masharubu aang'ono, iwo anabwera ku Rhodesia.

210 Woyendetsa ndege wamng'ono wosajaira anandiwulutsira mu umodzi wa mikuntho imeneyo, kenako anapita mailosi awiri zinkawoneka ngati, mmwamba mu mlengalenga, tikuzungulira zungulira. Sitimadziwa ngati tinali mozondoka; ndegeyo ikutembenuka ndi kutembenuka ndi kutembenuka. Ndipo potsiriza iyo . . . Sitimadziwa ngati iyo imapita pansi kapena mmwamba. Ndipo potsiriza iyo inatiponyera ife pamwamba pa mkuntho. Ndipo ndinadwala kwambiri mmimba mwanga pamene tinkatsika!

211 Angapo a atumiki amenewo, atumiki Achipentekoste, anakwera mu galimoto ndipo amandiyendetsa ine waku Pretoria. Ine ndinabwera kuchokera ku Southern Rhodesia; ndipo ine ndinafika kumeneko ndipo ine ndinali ndikudwala, mulimonse. Ndipo M'bale Baxter atakhala pamenepo,

akudwala, ndi Billy Paul, akudwala. Ndipo apa ife tinali tikuyendetsa kumatsika kudutsa mmanyumba; uko ndi kumene anthu achikuda amene amachita chinachake ankayenera kusiya fuko lawo, tchimo lina la fuko, ndipo iwo ankabwera mmenemo. Ndipo iwo samawalola iwo kubwera mu mzinda, kotero iwo ankangokhala mnyumba za zitini kapena chirichonse chimene iwo akanatha, zauve kwambiri ndi zinthu, ndi zoona. Ndipo uko iwo ankapita akudutsa kumeneko, ndipo ine ndinawona chikwangwani pamenepo, chinati, "Mailosi twente pa ora." Ndipo amuna amenewo ankayenda mailosi sikisite-faivi pa ora. Amayi okalamba osawuka amenewo akuthamangira kunja uko kukawagwira ana aang'ono amenewo, ana aang'ono, ali maliseche, kunja uko pa msewu, ndipo kuyambira pafupifupi usinkhu wa zaka ziwiri mpaka faivi kapena sikisi; kuwagwira ana aang'ono amenewo, ndi kumakuwa. Iye anafika pafupi ndithu kuti apha foro a iwo nthawi imodzi.

212 Ine ndinamugwira iye pa phewa, ine ndinati, "Hei! Vuto lako ndi chiyani?"

Iye anatembenuka, anati, "Inu mwati chiyani?"

213 Ine ndinati, "Ine ndinati, 'Vuto lako ndi chiyani?' Chepetsa liwiro la chinthu chimenecho!"

Anati, "Ife talamulidwa kuti tikakufikitseni inu kumeneko mu nthawi yake."

214 Ine ndinati, "Ine ndikukupatsa iwe malamulo kuti usiye zimenezo." Ndipo iye anati. . .Ine ndinati, "Kodi iwe ulibe kukhudzidwa kulikonse ndi anthu amenewo?"

"Anthu ake ati?"

Ine ndinati, "Ana aang'ono amenewo kunja uko amene unatsala pang'ono kuwagunda."

Anati, "Amenewo ndi a Kaffirs!"

215 Ine ndinati, "Manyazi pa iwe! Kumadzitcha wekha Mkhristu?" Ine ndinati, "Kodi iwe sukudziwa kuti mayi ameneyo amaganiza kwambiri za mwana wake, ngati iwe ukanamupha iye, monga amayi ako akanaganizira za iweyo?" Ine ndinati, "Iye akhoza kukhala mbuli ndi wosaphunzira, koma chikondi cha mayi chimalirira mwana wake. Iwe ulibe ntchito yochitira zinthu ngati zimenezo. Ndipo iwe umadzitcha wekha. . ." Ine ndinati, "Chinthu china, chikwangwani chija chinati 'mailosi twente pa ora,' Baibulo langa linati, 'Mupereke kwa Kaisara zimene ziri za Kaisara.'" Ndipo iye anagwedeza mutu wake. Ine ndinati, "Iwe uyichepetse iyo liwiro mpaka pa mailosi twente pa ora ndi kuwachitira anthu amenewo ngati kuti iwo anali m'bale wako." Ine ndinati, "Manyazi pa iwe, chirichonse chonga icho." Oh, mai, iwo anafufuma ngati achule akudya machaka! Koma izo sizinapange kusiyana kulikonse, ndinafikitsa mawu anga, nkhonya yanga.

216 Ndipo ife tinapita mozungulira pamenepo ndipo anthu anadziwa kuti ine ndinali wa mbali yawo, kuwabweretsera iwo—Nkhani ya Uthenga Wabwino. Ndipo Mulungu . . .

217 Iwo analowa mmenemo, ndipo anawasakaniza iwo, ndi kuyika azungu mbali imodzi, ndi achikuda, ndipo pamenepo achikudawo sankayankhula ngakhale liwu limodzi kwa iwo, kapena kalikonse. Mzimu Woyera unkapita pakati pawo ndi kutulutsa odwala ndi osautsika ndi olumala, ndi kuwachiritsa iwo, ndi kuwalola *iwo* kukhala cha kuno mmalo awo aakulu otsika atamangidwa kumeneko. Zimawonetsera momwe Mulungu amachitira ndi odzichepetsa mu mtima!

218 Tsopano, ameneyo ndi munthu amene sanalandirebe Uthenga ndipo akulemba bukhu limenelo.

219 Tsopano, kodi ine ndichite chiyani? Chinthucho, kodi ine nditani . . . Ndi—kodi ndikuyenera ndibwerere kumeneko? Tsopano, ngati Mulungu akundiyitanira ine ku uvangeli, ndiye ine sindingakhale mpenyi Wake ndi mvangeri pa nthawi yomweyo. Iwe basi . . . izo . . . Maudindowo sangasakanikirane, ndine—ndine basi . . . Ndikumenyana ndi mphepo. Ngati ine nditi ndidzakhale mvangeri, ine ndikuyenera kudzakhala mvangeri. Ngati ine nditi ndidzakhale mpenyi Wake, ine ndidzapita kumapiri kwinakwake ndi kukakhala kutali; wopanda tchalitchi, wopanda osonkhana, mpaka ine nditamva kuchokera kwa Ambuye; ndi kutulukako ndi kudzawupereka Iwo, ndi kumabwerera nso kachiwiri. Mukuona? Chimodzi mwa zinthu zimenezo, ndi kuyeza mu sikelo. Kapena mwinamwake izo zatha. Zikungoyenera kukhala chimodzi mwa zinthu zitatu zimenezo, kwa ine. Uthengawo watha kapena ine ndikuyenera kupeza chimodzi cha zinthu ziwiri izi zoti ndichite. Sindikudziwa choti ndichite.

220 Usiku wathawu ndinalota loto, ndipo ndinalota kuti ndimapita ku msonkhano, ndipo sindinaliwonepo gulu lotero la anthu! Iwo anasonkhana ngati m'bwalo lalikulu lamasewera, kutali momwe ndimawonera. Ndipo winawake amabwera akunditsatira ine amene sanali Billy, ndipo iye ananditengera ine kumusi. Ndipo ine ndinali ndiri mu chipinda, ndikupemphera, ndipo ndimabwera ku . . . pansi pa kudzodza; kukhala ngati mmene iwo amazitchulira izo, kukupangitsa iwe kuti umvetse, monga giya pamene ine ndikanakhoza kumverera kuti iko kukanakhala kuzindikira za mu mtima. Ndipo ndiri panjira kumeneko munthu wina anayamba kuyankhula kwa ine ndipo, pamene iye anatero, kuzindikira za mu mtima kunachokako. Ine sindimatha kukumverera iko. Ndipo kenako ine ndinayesera kudzikokera ndekha mmbuyo mu izo; ine sindinathe kuchita izo. Ine ndimalephera basi kuchita zimenezo. Ndipo ndinatopa.

221 Ndipo ndinayamba kuyang'ana pa khamulo pamene

linkayenda mokwera. Ndipo pamene ndinatero, ine ndinati, "Chabwino, ine ndiri ndi phunziro mmalingaliro mwanga limene ine ndikudziwa kuti mabungwe amenewo ndi momwe iwo ankachitira ndi anthu amenewo, ndiye ine ndilalikira Uthenga umenewo monga choncho kwa iwo mwamphamvu momwe ine ndingathere." Ndipo pamene ine ndinayenda kupita pa nsanja, izo zinandichokera ine.

222 Panalibe kuzindikira za mumtima, panalibe umodzi wa mauthenga amenewo; ndipo ine ndinayima pamenepo, ndipo komabe anthuwo anali akuyembekezera. Ndipo ine ndinati, "Kodi ndichite chiyani?"

223 Ndipo Chinachake chinati, "Uzingopitirira nazo. Uzingopitirira nazo, mwaona," izo zikaperekedwa ndikafika kumeneko. "Uzingopitirira kumasuntha." Mukuona? Kenako ine ndinali pomwepo pa nsa-. . . ndipo ine ndinadzuka.

224 Izo zikhoza kukhala chifukwa choti ndimaganizira zimenezo, ndinalota loto loterolo. Izo zikhoza kukhala zimenezo. Izo zikhoza kukhala kuti lotolo ndi lauzimu. Ine sindikudziwa. Ine ndiribe kutanthauzira kwa ilo, ine—ine sindikudziwa chimene ilo likutanthauza. Ine basi sindingathe kukuuzani inu ndipo ine—ine sindikudziwa chimene ilo liri. Koma, chirichonse chimene ilo liri, ine ndiri pa mphambano penapake. Mukuona? Pali chinachake, chinachake kwinakwake.

225 Ndipo ine—ine ndikhoza kunena chinthu chimodzi, ndipo ine sindimamvetsedwa bwino. Kapena ndinene mwanjira *iyi*, ine . . . ndi njira *iyi* kapena njira *iyo*, wina amazitengera izo kutali mbali *iyi*. Ndipo momwe izo ziriri, iwe umanena chinachake molunjika kumene pa mfundoyo, ndipo wina amamva Izo mwanjira *iyi*, kotero iye amamuuza wina ndipo amatsamira patsogolo pang'ono, ndipo wina amatsamira patsogolo pang'ono, wotsatira patsogolo pang'ono, ndiye Izo zimachoka pa mfundo yeniyeniyo. Wina amamva Izo mwanjira yina *iyi*, iye amapita njira iyi, njira iyo, ndi njira iyo. Mwaona, ndipo iwe umachokapo. Ndipo umo ndi momwe izo zimakhalira mu—mu misonkhano, ndi zina zotero, pamene iwe ukukhomerera kwenikweni pa Malopo. Tsopano, Osankhidwa amawamva Malo amenewo. Iwo amapeza Malo amenewo! Iwo amadziwa, chifukwa ine ndinanena ndendende basi chimene chimatanthauzidwa (Mukuona?) monga choncho, Uthenga basi, ndendende basi.

226 Tsopano, ndipo icho ndi chimene ine ndikunena, zikuwoneka ngati pali kusamvetsetsana kochuluka nthawi zonse, mosalekeza. Icho ndi chiyani? Ndi . . . Kodi ine ndabzala Mbewu zonse zimene zimayenera kubzalidwa? Kodi nthawiyo yayandikira? Kodi mtumiki wamkulu uyu akukonzekera kuti abwere powonekera pakali pano? Kodi kudza kwa Ambuye kuli pafupi? Kodi ndi kuyitanira kuchoka ku dziko lino kupita ku lina? Kodi Iye wandiyitana ine kuchoka ku uvangeli?

227 Inu mukukumbukira, ndine. . .Ndinazibwereza izo kwa mkazanga. Ambiri a inu mu bukhu. . .Tsiku limene ine ndinayika mwalawapangodya uwo kumeneko, pafupifupi zaka sarte zapitazo, apo pomwe pa ngodya, izo zinanenedwa mmenemo. . .Mmawa uja pamene Iye anandidzutsa ine, ndipo ndinali nditakhala mu chipinda uko, ngakhale ndisanakwatire nkomwe kapena chirichonse, mlaliki wachinyamata chabe, Iye anati, "Uchite ntchito ya mvangeri. Osati. . .Iwe sunali mlaliki, koma uchite *ntchito* ya iye," anabwereza Lemba kwa ine. Pamene ine ndinathamangira uko ndi kukawona mitengo iwiri imeneyo, ndinathyola umodzi kuchokera *apa*, umodzi ndi utatu. Ine sindinaikweranitse konse iyo, ine ndinaibzala iyo monga choncho. Ndiye Iye anawona chipatso chikugwera mdzanja langa ndipo kenako anandithamangitsira ine ku Kalvare. Tsopano mvetserani, Iye anati, "Pamene iwe utuluke mu izi, uwerenge Timoteo Wachiwiri 4, Timoteo Wachiwiri 4."

228 Ndipo Iwo anandisiya ine nditakhala mchipinda. Ine sindinkadziwa nkomwe kuti anali masomphenya. Ine sindinkadziwa kuti ndizitchule chiyani pamenepo. Ine ndinali ndikuyika mwalawapangodya (tsiku limenelo) wa maziko pamenepo. Izo zinalembedwa, ziri apo pomwe pa mwalawapangodya uwo tsopano, ndipo anati:

> . . .*ugwire ntchito ya mvangeri, upange kutsimikizira kwathunthu kwa utumiki* wako.
>
> *Pakuti idzafika nthawi imene iwo sadzapirira nacho chiphunzitso cholamitsa; koma motsatira zilakolako zawo adza. . .adzadziunjikira* kwa *iwoeni* pamodzi *kuphunzitsa—aphunzitsi, okhala ndi makutu oyabwa;*
>
> . . .ndipo adzachotsedwa ku Choonadi *kupita ku nthano*. (Ndizo ziwiri zonse umodzi ndi utatu, iwo aphonya a. . .)

229 Tsopano, Iye sananene konse "iwe ndi mvangeli," Iye anati, "Uchite *ntchito* ya iye." Mukuona? Tsopano, kodi nthawiyo yafika? Ndipitirize ndi zimenezo kapena nthawi yafika ya chinachakenso? Zimenezo ine sindikuzidziwa.

230 Izo ndi zomwe ine ndimafuna, kuyankhulana kwa mtima-ndi-mtima ndi inu. Ndipo ndadutsitsa nthawi yanga pakalipano, yokulolani inu kuti muzipita, pepani pokusungani motalikitsa chomwecho.

231 Koma, ngati Ambuye alola, M'bale Boze asanabwere Lamlungu, ine ndikhoza kudzabwera Lamlungu mmawa ndipo ndikhoza kudzayankhula pa mutu wa *Uvangeri Wa nthawi-Yakumadzulo*, kapena chinachake chonga icho, mwaona, ngati izo. . .Kodi izo ziri bwino ndi inu, Abusa? [M'bale Neville akuti, "Nzabwino! Mulungu alemekezeke!"—Mkonzi]. Ambuye akalola, Lamlungu lotsatirali mmawa. Ndipo ine ndimati ndidzayankhule pa zimenezo usikuuno, ndipo ine

ndimati ndikhale ndi kuyankhulana kwa mtima-ndi-mtima mwinamwake nthawi ina, koma ine ndikumverera kuti izo zingakhale zabwinoko mwanjira iyi, mwinamwake, mwaona, ngati icho chingakhale chifuniro cha Ambuye.

232 Ine ndizikupempherani inu. Inu muzindipempherera ine. Basi osati—osanena kuti, "M'bale Branham, ine nditero." Inu muchite zimenezo! Mukuona? Ine ndikudalira pa zimenezo. Ine ndi amene ndikusowa pemphero, ngati Iye angandikankhire ine kwinakwake. Kumbukirani, ndine munthu, ine si Mulungu. Ndine munthu basi monga inu muliri, ndikuyesetsa kuti ndipeze chifuniro cha Mulungu kuti ine ndizikhoza kumayenda mu icho. Palibe amene angadziwe mpaka. . . "Ndipo iye amene alibe nzeru apemphe kwa Mulungu." Ndipo icho ndi chimene ine ndikuchita, ndikupempha kwa Mulungu. Ndipo ine ndikungoyika izo kwa inu ngati mpingo wanga, kuyankhulana kwa mtima-ndi-mtima. Chiyani, kodi ife tiri pati? Kodi ife tayima pati? Kodi ife tikukhala mu ora liti? Ife tiri ku mapeto a nthawi, ine ndikukhulupirira. Ine ndikukhulupirira kuti ife tiri pomwe pano pamapeto.

233 Tsopano, izo zikhoza kutembenukira njira imodzi kapena imzake. Kotero inu. . .Mwinamwake ndi zakuti ntchito yanga yatha, kapena ndikuitanidwira ku ntchito kutsidyako, kapena mwinamwake Iye adzampanga mvangeri kapena mpenyi. Chimodzi cha zinthu zimenezo chikuyenera kuchitika, chifukwa ine ndiri kumapeto. Ine sindikudziwa choti ndichite. Ine sindikudziwa njira yoti ndipiteko. Ngakhale misonkhano iyi, imene ine ndikuyiyandikira iyo, ine ndakhala ndikupemphera, ine ndinati, "Ambuye, ine sindichita monga ndakhala ndikuchitira. Ine ndizifikira izo monga ine ndinkachitira kumbuyo uko, ine ndibwerera ku uvangeli umenewo mpaka Inu mutandipatsa ine kuyitana kumeneko pa zomwe ine ndikuyenera kuchita."

234 Ine nda—Ine ndafesa Mbewu kulikonseko, matepi apita padziko lonse, Mauthenga anga apita kuzungulira dziko lapansi, mipingo yonse ikudziwa za Iwo, kuzungulira kulikonseko, ndipo amene Atate anawasankha Iye adzawaitana iwo. Mukuona?

235 Ndipo tsopano izo zikuwoneka ngati Iwo ukukhala mlandu kwa iwo. Oh, iwo sakufuna kanthu kochita ndi Iwo. Ayi, bwana. Kodi ndingopita ndi kukapempherera odwala, ndi uthenga wophweka waung'ono pa izo, ndi—ndi kuwona momwe Mzimu Woyera unditsogolere ine? Icho ndi chimene chiri mmalingaliro anga kuti ndichite mpaka Iye adzapange kuyitana kwina. Chifukwa munthu samadziwa choti achite mpaka utamvetsa kuchokera kwa Mulungu choti uchite, mpaka utapeza pamene iwe uli.

236 Ndipo ine—ndipo ine sindikufuna kuti ndizikhala panyumba. Uthenga uwu uli pa mtima wanga. Anthu akufa,

akugwa, akupita ku Muyaya. Kodi ndichite chiyani? Mundirole ine ndiwuphulitse Iwo kulikonse kumene ine ndingathe, ndi kunena za Ambuye Yesu mpaka Iye atasintha malo. Inu mundipempherere ine, ine ndikupemphererani inu. Ine ndikuyembekeza kuti inu muchita zimenezo.

237 Tsopano, kumbukirani Lachitatu usiku, msonkhano wa pemphero, ndi Lachisanu usiku, msonkhano wa amuna. Kodi iwo udzakhala kuno? Ine ndikhoza kudzakhalapo kuti ndidzakuwoneni inu nonse, ine ndinakuuzani kuti ndidzabwera kudzakuwonani Lachisanu usiku. Chabwino, ndiye Lamlungu mmawa, Ambuye akalola, ine ndidzayankhula pa *Uvangeri wa Nthawi Yakumadzulo*, ngati Ambuye alola; ndikhoza kudzawusintha iwo, sindikudziwa. Koma izo ndi zomwe ine ndikuziganizira pakali pano, mtundu wa avangeri amene adzakhale mu nthawi ya kumadzulo. Ndipo kenako Lamlungu usiku, filimu ya M'bale Boze, ndipo muzikumbukira zimenezo tsopano. Ndipo mutipempherere ife, pakuti sabata yamawa ife tidzagunda mmunda wokolola, Ambuye akalola.

*Kodi inu mumamukonda Iye?* Ameni!
*Kodi inu mumutumikira Iye?* Ameni!
*Kodi inu mumukhulupirira Iye?* Ameni!
Ameni! Ameni!

*Iye ndi Atate*. Ameni!
*Iye ndi Mwana*. Ameni!
*Iye ndi Mzimu Woyera*. Ameni!
Ameni! Ameni!

*Tikuyimbabe*. Ameni!

Ameni! Ameni! Ameni! Ameni!

*Kodi inu mumamukonda Iye?* Ameni!
*Kodi Iye akubwera?* Ameni!
*Kodi inu mwakonzeka?* Ameni!
Ameni! Ameni!

*Zikhoza kukhala usikuuno, kodi inu mwakonzeka?* Ameni!
*M'mawa, kodi inu mwakonzeka?* Ameni!
*Nthawi iliyonse, kodi inu mwakonzeka?* Ameni!
Ameni! Ameni!

*Tikuyimbabe*. Ameni!
*Ndi kufuula*. Ameni!
*Ndi kupemphera*. Ameni!
Ameni! Ameni!

*Bwerani Ambuye Yesu*. Ameni!
*Konzekeretsani Mpingo Wanu*. Ameni!
*Tikukonzekera*. Ameni!
Ameni, Ameni!

*Ndikufuna kukawawona amayi anga.* Ameni!
*Ndikufuna kukawawona bambo anga.* Ameni!
*Ndikufuna kukamuwona Mpulumutsi wanga.* Ameni!
Ameni! Ameni!

*Oh, kodi inu mumamukonda Iye?* Ameni!
*Kodi inu mumutumikira Iye?* Ameni!
*Kodi inu mumamukonda Iye?* Ameni!
Ameni! Ameni!

238 Atate athu a Kumwamba, iyi ndi yathu . . . nyimbo ya *Ameni* yaying'ono. Ife timakonda chiphunzitso Chanu, ife tonse tikuti "Ameni!" Ife timakonda Mzimu, "Ameni!" Ife tikukhulupirira kuti Iye akubwera, "Ameni!" Mawu aliwonse amene Inu mumayankhula mu Baibulo Lanu, Ambuye, ife timawavomereza Iwo ndi "Ameni!" Ife timakhulupirira Mawu aliwonse a Ilo, kuwaphunzitsa Iwo mwakupambana kwa kudziwa kwathu, basi momwe Iwo analembedwera, kalembedwe kalikonse, cholumikiza chirichonse, mpumiro uliwonse, cholekanitsa chirichonse, momwe Iwo basi analembedwera, mwa kupambana kwa kudziwa kwathu.

239 O Mulungu, bwezeretsani kwa ife, Ambuye. Perekani kwa ife kukhutitsidwa kwakukulu kumene ife tikukufuna, kuti ife tsiku lina tidzamve kuwomba kwa Angelo pamene iwo azidzatulukira mu nyimbo ya Aleluya mu mlengalenga, monga Yesu adzawonekera kutsidyako ndipo Mpingo udzakwatulidwira mmwamba.

240 Osakhulupirira adzadabwa, "Chachitika ndi chiyani, chavuta ndi chiyani ndi anthu amenewo? Kodi iwo apita kuti?" O Mulungu, iwo sadzamvetsa, iwo sadzamuwona nkomwe Iye. Koma Mpingo udzamuwona Iye, ndiko kuti, oyitanidwa-atuluke, Osankhidwa, obadwa- mwatsopano, iwo adzangosowa. Iwo sadzadziwa kumene iwo ali, iwo adzangodziwa kuti akusowa; iwo adzakhala ali ndi Ambuye wawo.

241 Ndiye pa nthawi imeneyo, Ambuye, kodi sichidzakhala chinthu chowopsya kudzasiyidwa kuno, podziwa kuti nthawi ya chipulumutso yapita? Palibenso chiwombolo! Lemba linati, "Musiyeni iye amene ali woyipa akhalebe chiyipire, musiyeni iye amene ali wosayera akhalebe wosayera." Oh, ilo lidzakhala ora lotani!

242 Mulole ife tikonzekere tsopano, Ambuye. Iyo idzakhala nthawi yopambana bwanji ngati tidzangokonzekera kudzakumana ndi Inu, Atate, ndi kukonzekera mitima yathu tsiku ndi tsiku. Ndipo ngati ife tilakwitsa ndi kugwa, monga moyo wosauka uwu unalembera mu funso ili lero, aloleni iwo adziwe kuti Magazi a Yesu Khristu amatsuka tchimo lonse. Munthu ameneyo sakutanthauza kuti achite zimenezo, Ambuye. Iwo akuchita njala ndi ludzu, akuyesetsa kuti abwerere mu

chiyanjano chimenecho cha Mzimu. Abweretseni iwo, Ambuye. Adzutseni iwo pamwamba pa dziko la mitambo, lolunda ili; pamwamba, kumene kuwala kwa Dzuwa kukhoza kuwalira pa miyoyo yawo kachiwiri. Iwo atsikira pansi mmusi mwa—a—gawo lalikulu la—la mitambo, ndipo iwo ali pansi mmatope, pansi mu tchimo limenelo. Koma iwo anakhalapo mmwamba kumeneko mu kuwala kwa Dzuwa. Iwo—iwo akufuna kubwerera kachiwiri, Ambuye. Abwezeretseni iwo usikuuno, Ambuye. Ndipo ngati pali ena pano amene sanachitirepo umboni wokhala pamwamba apo, ndipo akudziwa kuti . . .

243 Mizinga yonse iyi apa ndi chirichonse chiri ndendende basi mogwirizana ndi Mawu Anu, ndendende basi momwe zinthu zikuyenera kuchitikira. Ndipo ife tikuwona kuti dziko la mpingo, momwe iwo achitira izo. Ife—ife tikuwona basi—monga izo zinali mmasiku a Nowa, monga izo zinali mmasiku a Sodomu, ndendende basi chimene Yesu ananena kuti zikanadzachitikira, mafunde amphamvu, momwe akazi azidzayendera ndi kuvala, ndi momwe iwo akanati adzakhalire odedeluka, ndi—ndi kumayenda, chabwino, momwe iwo akuchitira, ndi kumanjanja ndi kumadzithyola, ndi kumapitirira, ndendende basi chimene mneneri ananena. Basi zomwe Daniele ananena, "Chitsulo ndi dongo sizingagwirizane pamodzi." Ndipo, oh, chirichonse, izo zakwaniritsidwa, Ambuye. Ife tiri pa nthawi yakumapeto. Mithunzi ikugwa, Ambuye. Magetsi ofiira akuthwanima, mabelu akulira.

244 O Mulungu, mulole anthu Anu azindikire kuti posachedwapa Mngelo adzaponda pa mtunda ndi panyanja ndi kudzakweza mmwamba manja Ake ndi kudzati, "Nthawi sidzakhalaponso!"

> Ndiye O, kulira ndi kusisima kotani,
> Pamene otayika adzauzidwa za tsoka lawo;
> Iwo adzalirira kwa miyala ndi mapiri,
> Iwo adzapemphera, koma pemphero lidzachedwa kwambiri.

245 Lero ndi tsiku la chipulumutso. "Muloleni iye amene ali ndi khutu amve chimene Mzimu akunena kwa mipingo." Perekani izi, Ambuye.

246 Mulole pasakhale munthu mmodzi pano amene adzasowe pa tsiku ilo la Mkwatulo. Mulole ife tikhale odzazidwa ndi chikondi cha Mulungu ndi Mzimu wa Mulungu mpaka Mzimu Woyera udzatitengere ife kutali ndi kumakadikirira, kapena ngakhale ife titadzapuma pamalo athu. Monga Inu munanena kwa Daniele, "Pita njira yako, Daniele, pakuti iwe udzapumula. Koma pa tsiku limenelo iwe udzayima pamalo ako."

247 O Mulungu, Inu munati, "Iwo amene amatembenuza ambiri kwa . . . kuchoka ku tchimo kupita ku chirungamo adzawala kuposa nyenyezi kwa nthawi za nthawi." Ndi tsiku lotani! Koma

oyipawo adzatembenuzidwira ku chiwonongeko. O Mulungu, mupangeni munthu kuti azindikire malo ake pakali pano m'moyo, kuti iwo atembenukire kwa Wolungama Mmodziyo nthawi isanathe kwanthawizonse. Perekani izi, Atate.

248 Tsopano ndi mitu yathu yoweramitsidwa mphindi chabe, mu pemphero lotsekera, kodi pangakhale mmodzi akufuna kuti akumbukiridwe, akuti, "M'bale Branham, ine ndakweza dzanja langa, osati kwa inu koma kwa Mulungu. Mulungu andichitire ine chifundo ndipo ine ndidzakhalapo pa tsiku limenelo, wosambitsidwa mu Magazi a Mwanawankhosa"? Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, inu, inu, inu, inu, manja ambiri.

249 Tsopano, Atate Mulungu Wakumwamba, mudalitse aliyense, mmodzi aliyense. Inu mwawona manja awo. Inu mukudziwa mitima yawo.

250 Ndipo ife tikuzindikira, Ambuye, kuti ife. . . chinachake chikukonzekera kuchitika. Dziko likudziwa zimenezo, iwo akuyimba nyimbo, ndipo matelevizioni akuphulika ndi nthabwala ndi nyimbo zamisala. Kodi iwo akuchita chiyani? Monga mnyamata wamng'ono akuyimba mluzu mu mdima, akudutsa pamanda, ali ndi mantha kuwopa kufa, akuyesetsa kutontholetsa mitsempha yake poliza mluzu. Iye akungodzipusitsa yekha. Chomwechonso fuko lino likungoseka, kusereula, kusewera, monga momwe Iwo ananenera kuti nthawi ikanadzafika pamene iwo akanati adzachite zimenezo, "Kutembenuzidwa kuchoka ku Choonadi kupita ku nthano," ndi momwe kuti "m'masiku otsiriza kukanadzabwera onyoza ndi oseka," ndi momwe zinthu izi zikanadzakhalira pa nthawi yakumapeto, "odzimva, odzikuza, okhala ndi mawonekedwe achipembedzo, kuchoka ku Choonadi," ndipo ife tikuziwona izo pakali pano.

251 O Mulungu, adzutseni anthu! Aloleni iwo azindikire kuti iwo akhoza kukhala otsimikiziridwawo pakali pano kuti iwo adutsa kuchoka ku imfa apita ku Moyo. Pamene ife tilandira Khristu, Mzimu Woyera, ife timangokwera pamwamba pa dziko. Ndiye ife timadziwa kuti taukitsidwa kale ndi Iye, ndipo tikungoyembekezera kusintha kumeneko kumene imfa idzatha mmadera a chivundi, magudumu aang'ono awa a moyo wachivundi amene akuzungulira mu mphamvu zathu, adzawomboledwa. O Mulungu! Ndiyeno ife tidzakhala ndi thupi ngati Lake ndipo tidzakhala Mwamuyaya ndi Iye, Dziko lalikulu lolonjezedwa, kukhala ndi Umboni.

252 Musalole wina aphonye zimenezo, Ambuye. Iwo amene anakweza manja awo, mulole iwo asese (usikuuno) kulowa mu Ufumu. Mwinamwake iwo akamapita kwawo, mwinamwake mwamunayo akamuuze mkazi wake, "Wokondedwa, chinachake chandikhudza ine usikuuno"; kapena mkazi akanene kwa

mwamuna wake, "Wokondedwa, ine—ine ndinamverera mwachilendo kwenikweni." "Inde, wokondedwa, tiye tigwade apa pambali pa bedi. Ife sitinachitepo izi kale, koma tiye ife tipemphere usikuuno. Tiye timupemphe Mulungu kuti atichitire chifundo ndi kutisonkhanitsa ife. Ine ndimakukonda, wokondedwa."

253 Ndipo a—winayo, mwamuna kunena kwa mkaziyo, ndi momwe iwo amakonderana wina ndi mzake, "Ine—ine—ine ndikufuna kukakhala Kumwamba ndi iwe. Ine sindikufuna kuphonya zimenezo. Ndipo tsiku lina pamene ife tidzalandiridwa Kwathu ndipo ine ndidzakugwira iwe pa nkono ndipo tidzayenda kupyola mmakolido aakulu ndi minda Yamuyaya, kumene mwanawankhosa ndi—ndi mkango zidzagona pamodzi, ndipo nkhandwe ndi a—ng'ombe zidzagona pamodzi. Ndipo sikudzakhalanso imfa ndi chisoni. Ndipo pamene ife tizidzayenda kudutsa kumeneko ndipo nyimbo za fuko zikudzaza mmlengalenga, za Angelo, nyimbo pamwamba pathu, pamene Angelo azidzatilandira ife Kwathu, ine ndikufuna kuti ndidzakhale ndi iwe kumeneko, wokondedwa. Ine—ine ndimakukonda iwe. Mwinamwake iwe ukukalamba, ndikukumbukira pamene ndinakukwatira iwe, nkhope yako yaying'ono yokongola." "Ndipo—ndipo iwe, ndipo ine ndikukumbukira iwe, wokondedwa, pamene iwe unali mnyamata wokongola."

254 Koma zonsezi zidzabwezeretsedwa. Iye Amene anajambula nkhope yako yokongola nthawi ina ali ndi—ndi mawonekedwe a iyo mmalingaliro Ake. Iye akhoza kuijambula iyo kachiwiri kutsidyako kumene iyo siidzazimirira konse. O Mulungu, aloleni anthu adziwe kuti ili si loto lanthano, koma ndi—Choonadi, ndipo Mulungu, Mzimu Woyera, uli pano kuti uchitire umboni. Mawu Ake kudutsa mmibadwo anayankhula za izo. Tiyeni tiyang'ane mmbuyo ndi kuwona, tiwerenge mbiriyakale yathu. Ndipo munthu aliyense amene anafika pokhala chirichonse padziko lapansi ndi munthu, munthu wowopa Mulungu, ngakhale kwa Mapurezidenti athu monga Washington, Lincoln, ndi ena otero, *Joshuas*, ndipo—ndipo kenako. . .*Moseses*, ndi iwo amene. . .Anthu otchuka apa dziko lapansi akhala anthu amene amakhulupirira mu zimenezo, ndipo anasindikiza umboni wawo, ndipo akuyembekezera kutsidyako chiwukitsiro chimenecho. Ife tiri ndi zipatso zoyamba za izo, Chikole.

255 Ine ndikupemphera tsopano kuti kupyolera mu pemphero langa Inu muwalandire anthu awa ndi pemphero lawo ndi kuwatengera iwo mu Ufumu. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

256 Mulungu akudalitseni inu, akhale wolemera mu chifundo kwa inu, apangitse nkhope Yake kuwala pa inu, ndi kukusungani inu, ndipo akudalitseni inu mu madalitso onse a Kumwamba.

257 Tsopano ndikunena ichi, osati mwankhanza, koma mwachikondi. Ndikupemphera kuti inu amene simukumudziwa Iye, kuti chotsamira chanu chikakhale cholimba kotero kuti musakathe kugonanso, chakudya chanu chikakhale choyipa kwambiri mpaka musakathenso kudya, mpaka mukazembere kumbali kwinakwake ndikuti, "Ambuye, mundichitire ine chifundo." Uko sikufunira chirichonse cholakwika kwa inu. Izo ndi za ubwino wanu, m'bale, mlongo. Ine ndikungopemphera kuti zikakhale mwanjira imeneyo kwa inu.

Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!
Mpaka tidzakomane pa mapazi a Yesu; (Mpaka tidzakomane!)
Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!
Mulungu akhale nanu mpaka tidzakomanenso!

Mulungu akhale nanu mpaka tidzakomanenso!
Ndi uphungu Wake akutsogolereni, akuchirikizeni,
Akanthe mafunde owopsya pamaso panu;
Mulungu akhale nanu mpaka tidzakomane . . .

258 Tsopano chifukwa cha nthawi yakale, tiyeni tigwirane chanza ndi winawake tsopano.

Mpaka ife . . .

Ambuye Yesu, pangani . . . ? . . . wathunthu, chotsani matendawo ndi kumuchiritsa iye, Ambuye, mu Dzina la Yesu.

Mpaka tidzakomanenso pa mapazi a Yesu; (Mpaka tidzakomane!)
Mpaka ife . . . ? . . .

Mpaka ife . . .
. . . a Yesu . . .

259 Inu mukukumbukira ife tinkakonda kuyimba nyimbo zimenezo? Tiyeni . . . Ndipo ina iyi imene ife tinkakonda kuyiyimba, zaka zambiri zapitazo, ine sindikudziwa ngati alipo ena pano kapena ayi, pamene ife tinkakonda kugwirana manja mozungulira mbaula yakale apa, ndi matope pansi. Inu mukukumbukira izo? Ife tinkayimba:

Tikuguba wa ku Zioni,
Wokongola, wokongola Zioni;
Tikuguba kumka mmwamba ku Zioni,
Mzinda wokongola Uwo wa Mulungu.

260 Inu mukudziwa mu Zakachikwi chimene Zioni ati adzakhale? Padzakhala Kuwala pa Zioni, ndipo kudzakhala kwa mthunzi wochokera kudzuwa masana ndi Kuwala usiku, pakuti sikudzakhala usiku kumeneko. Oh, mai!

Minda ya Zioni imapereka
Zokoma zopatulika sauzande
Tisanaufikire Mpandowachifumu
Wakumwamba uja,
Tisanaufikire Mpandowachifumu
Wakumwamba uja,
Kapena kuyenda m'misewu yagolide,
Kapena kuyenda m'misewu yagolide.

Tonse pamodzi tsopano:

Tikuguba wa ku Zioni,
Oh, wokongola, wokongola Zioni;
Tikuguba kunka mmwamba ku Zioni,
Mzinda wokongola Uja wa Mulungu.

261 Ndimangozikonda zimenezo, ndikungoganiza kuti izo ndi zokongola kwambiri. Tsopano, kodi inu simukuzikonda nyimbo zachikale zimenezo? Ndikuganiza kuti ndizabwino kwambiri kuposa zodulidwa izi zimene tiri nazo lero zotchedwa nyimbo. Ine ndimangozikonda zimenezo. Ndipo ine ndinkakonda kuyimba nyimbo yakale mu tchalitchi, inu mukukumbukira:

Malo, malo, inde, pali malo,
Pali malo pa Kasupe a inu.

262 Oh, mai! Nyimbo zabwino, zakale zimenezo, ine ndikukhulupirira cholemberacho chinkatsogozedwa ndi Mzimu Woyera, Umene unalemba nyimbo zimenezo.

Pafupi, Mulungu wanga, kwa Inu, pafupi kwa
Inu!
Ngakhale uli mtanda umene umandikweza ine.

263 Komabe, Charles Wesley ndi olemba opambana amenewo amene analemba nyimbo zimenezo monga choncho, andakatulo amenewo. Izo ndi zokongola, ndikungoganiza kuti izo ndi zabwino kwambiri. Ndipo kenako ife tinkakonda ku. . . Mukuyikumbukira ijayi:

O Dziko la Mtendere, Dziko lokoma la
Mtendere,
Pamene ine ndaima pamwamba pa phiri
lalitali kwambiri,
Ndikuyang'ana kutsidya la nyanja,
Kumene nyumba Inu mwandikonzera ine.

264 Mukukumbukira nthawi yoyamba imene Mngelo wa Ambuye anawonekera kumusi pa mtsinje? Ife tinali tikuyimba:

Mmagombe a mkuntho a Yordano ine ndayima,
Ndi kuponya diso lolakalaka,
Ku dziko la Kenani labwino ndi losangalatsa,
Kumene kuli chuma changa.

Ndikupita ku dziko lolonjezedwa limenelo,
Ndani ati abwere ndi kupita nane?

Ndikupita ku dziko lolonjezedwa limenelo.

265 Pamene ife tinali kuyimba iyo, Liwu linafuula kuchokera mumlengalenga, ndipo apa panabwera Lawi la Moto lalikulu lija likuzungulira mpaka pansi ndipo linati, "Monga Yohane M'batizi anatumidwa kuti adzatsogolere kudza Kwake koyamba, iwe uli ndi Uthenga umene uti udzatsogolere Kwachiwiri." Onani kumene iye wapita. Ndizo zaka sarte-wani zapitazo. Yang'anani kumene Iwo unapita kuchokera pamenepo, kuzungulira dziko mu moto wa chitsitsimutso. Ndipo tsopano ife tikuziwona izo zikuzizira. Nthawi yayandikira.

266 Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano, kukumbukira zolengeza zonse.

267 M'busa Wamkulu wa gulu la nkhosa, amene ife tikuyang'ana kuti tidzamuwone akubwera tsiku lina, mitima yathu ikuyembekezera ora limenelo pamene ife tidzamuwona Iye. Tsiku lina Inu munakhala pa phiri ndipo Inu munawaphunzitsa anthu Anu, Inu munati, "Muzipemphera motere:"

Atate athu Amene muli Kumwamba, Dzina Lanu Liyeretsedwe.
Ufumu Wanu udze. Kufuna kwanu kuchitidwe pa dziko, monga ziriri Kumwamba.
Mutipatse ife lero chakudya chathu cha lero.
Ndipo mutikhululukire ife zolakwa zathu, monga ife tiwakhululukira iwo amene atilakwira ife.
Ndipo musatitengere ife kokayesedwa, koma mutipulumutse ife kwa woyipayo; pakuti Wanu ndi Ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemelero, kwanthawizonse. Ameni.

268 Baibulo linati, "Ndipo iwo anayimba nyimbo, ndipo anatuluka."

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Mwana wachisoni ndi watsoka;
Lidzakusangalatsa ndi kukutonthoza,
Tenga Ilo kulikonse kumene upita.

Dzina lofunika, O kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo cha Kumwamba;
Dzina lofunika, O kukoma kwakeko! (Kukoma kwakeko!)
Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo cha Kumwamba.

269 Kodi zimenezo sizikumveka bwino? Mungolola kamodzi, imodzi yokha apa ndi apo, ndipo mvetserani kwa iyo kachiwiri pamene ife tikuyimba:

Pa Dzina la Yesu kuwerama,

Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake, (Mukuona?)
Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka Iye korona,
Pamene ulendo wathu udzatha.

Oh, kodi izo si zokongola? Tiyeni tiwone:

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Ngati Chishango ku msampha uliwonse;
Pamene mayesero akuzingani,
Mungopuma Dzina Loyeralo mu pemphero. (Mukuona?)

O Dzina lofunika! Tiyeni tiyimbe iyo:

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Ngati Chishango ku msampha uliwonse;
Pamene mayesero akuzingani,
Pumani Dzina Loyeralo mu pemphero.

Oh Dzina lofunika, (Dzina Lofunika!) O kukoma kwakeko! (O kukoma kwakeko!)
Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo cha Kumwamba;
Dzina lofunika, O kukoma kwakeko! (Kukoma kwakeko!)
Chiyembekezo cha padziko ndi chisangalalo cha Kumwamba.

270 Tsopano, ngati ife tingaweramitse mitu yathu, abusa athu abalalitsa osonkhana mu pemphero. Mulungu akudalitseni inu, M'bale Neville.

62-0527 Mafunso ndi Mayankho
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org